


TRUTH
CENTERED
TRANSFORMATION

MODULE



MCHERE NDI KUUNIKA BUKU LA MPHUNZITSI

Truth Centered Transformation—BUKU: MCHERE NDI KUUNIKA v4. Copyright ©2020^[1]Reconciled World, Phoenix, Arizona, United States of America. www.reconciledworld.org

Ntchitoyi yakhala yotheka pansi pa mgwirizano wa the Creative Commons Attribution–ShareAlike 3.0 license. Muli wololedwa komanso kulimbikitsidwa kugwiritsa ntchito,kukopera, kugawa ndiponso kufalitsa potsatira malamulo ali mmunsimu:

Kuthokoza – Muwonetsetse kuti pogwiritsa ntchito,kukopera,kugawa ndiponso kufalitsa zolembedwazi musaiwale kulemba kuti: Copyright © 2017. Published by Reconciled World (www.reconciledworld.org)Pansi pamfundo za the Creative Commons Attribution–ShareAlike 3.0 license.Ngati mufuna kudziwa zambiri , onani www.creativecommons.org.

Osagulitsa –Osapanga malonda ndi ntchitoyi.



Ngati muli osangalasidwa kuti mumasulire kabuku aka, chonde funsani ku info@tctprogram.org.

Mau onse a Mulungu amene ali mu bukuli atengedwa kuchokera ku buku lopatulika la mulungu imene inalembedwa ndi, New International Version®, NIV®. Copyright ©1973, 1978, 1984, 2011 by Biblica, Inc.TM. Used by permission of Zondervan. All rights reserved worldwide. www.zondervan.com. The “NIV” and “New International Version” are trademarks registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc.TM.

Musanayambe

Kukonzekera Phunziro loti mukaphunzitse

1. Werengani bukhu lonse la Mphunzitsi mosamala , kangapo ngati mkotheke. Lembani pambali zinthu zofunika zomwe mwatolapo. Izi zidzakuthandizani kuzikumbutsa nokha za zinthu zimene munawerenga.
2. Taonani mfundo zenizeni za phunziro lina lililonse cholinga choti mudziwe kuti ophunzira akuyenera kuphunzira pomaliza pa phunziro lonse.
3. Werengani chile malemba a mbaibulo amene akufunika kuti agwirizane ndi nkhanayi nthawi isanakwane.
4. Yang'anani ndi kuona kuti kodi ndi zipangizo ziti zomwe mungafunikile ndipo muonetsetsenso kuti mwachulukitsanso mabuku a ophunzira ndikukonza zithunzi zofunikila kuti zigwiritsidwe ntchito mu phunziroli.
5. Onetsetsani kuti mukunvetsetsa ndi kutsatila bwino chochitika china chilichonse (masewero , ma gemu , ndi zithunzi). Mukhoza kuziyesera ndi anzanu ena kapena banja lanu).
6. Tengani nthawi yopempherera ndikukonzekera komanso kupempherela ophunzira anu kuti Mulungu awakonzekeretse kuti amve chimene Mulungu akufuna iwo atamva , ndikuti iye akuthandizeni kuti mupeleke phunziro limeneli bwinobwino kuti anthu afike posintha.

BUKHU LA MPHUNZITSI

MFUNDO ZENI ZENI NDI ZIPANGIZO: Phunziro lina lililonse limayamba ndi ndime imeneyi.

1. **Mfundo zazikuluzikulu**– Pali mfundo zazikulu zambiri mu phunziro lina lililonse , koma ophunzira akuyenera kumvetsetsa mfundozi pakutha pa phunziro lina lililonse. Ndi bwino kuzifunsa nokha ngati mukuganiza ngati ophunzira anu akukumbukila mfundo zimenezi mukatha kuphunzitsa phunziro limeneli. Tengani nthawi kuunikila mfundo zenizeni kuti ziwathandize iwo kukumbukila mfundozi.
2. **Zipangizo** – Zipangizo zapadera zofunikila zimalembedwa pa phunziro lina lililonse , kuphatikiza zithunzi komanso mabuku aphunzitsi . bukhu la mphunzitsi lizaonetsera kuti ichi chigwiritsidwe ntchito pati:-
 - a. **BUKHU LA OPHUNZIRA** – Lizalembedwa moteremu.
 - b. **ZINTHUNZI** – Lizalembedwanso ngati choncho.

ZITHUNZI

Zithunzi zokhudzana ndi phunziro limeneli lili mu bukhu lapadera . tulutsani(printi) zimenezo monga mmene bukhu la zithunzi laperekela malangizo ake.

BUKHU LA OPHUNZIRA

Ngati gulu lanu silinalandile bukhu lonse la ophunzira , chulukitsani ndikumpatsa wina aliyense ma pepala omalizila amene ali pamapeto pa bukhu la aphunzitsi:.

1. Phunziro 6: kugonjetsa tchimo- machimo amene amachitikachitika.
2. Phunziro 7: Pulani yakatumikilidwe kanga.

PHUNZIRO 1: MCHERE NDI KUUNIKA

Mfundo zeni zeni:

- Monga mhere , miyoyo yathu ili ndi cholinga choti ikabweretse kusintha potizungulira ndi dera lathu.

Zipangizo

- Zithunzi : ” sindingathe kupanga masamu;; sewero(ma kope atatu amene akufunika).
- Choikilamo cha mchere.
- Buku la ophunzira : nkhani zitatu zopeka

CHIYAMBI: Mchere

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU.

MALANGIZO KWA APHUNZITSI : Ikani madzi mu komtena ndi mchere mkati mwake kapena yendetsani mchere mkati mwa chipindachi kuti anthu aone.

- Kodi ichi ndi chani?
- Kodi chimagwira ntchito yanji?. Kuteteza chakudya kuti chisaonongeke , kuyeretsera , kusamalira.

Mchere ndi njira yoyamba komanso yodabwitsa yopangila zinthu kukhala bwino! Makamakanso , mchere ndi ofunikila pa matupi athu , sitingakhale opanda mchere.

Yesu ananena za mchere monga chizindikiro cha chimene a khristu ali. Lero tikufuna tione mmene tingakhalire mchere umenewu mmadera mwathu. Tatiyeni tiyambe ndi kuona malemba kuti tipeze chomwe yesu ananena zokhudzana ndi mchere.

NDINU MCHERE

KUKAMBIKANA KWA MMAGULU ANG’ONO ANG’ONO.

Werengani mateyu 5:13 ; ” Inu ndinu mchere wa dziko lapansi . Koma ngati mcherewu utaya kukoma kwake , kodi uzabwezeretsedwanso bwanji?. Udzakhala opanda mchito pa china chilichonse , kupatula kuti utengedwe ndikukatayidwa ndikuponedwa pondedwa ndi anthu.

Mu ndime imeneyi , Yesu akuyankhula ndi otsatila ake. Kuti ifenso ndife otsatila a yesu , iyenso akutilankhula ife. Mu nthawi ya yesu , mchere umawerengedwa monga chinthu chopambana kwambiri ndi cha mtengo wapatali- Chinali cha chuma chachikulu. Yesu akulowa ophunzira ake kuti adziwe kuti iwowo ndi a mtengo wapatali.

KHALANI NGATI MCHERE

Mchere unali komanso uli wa mtengo wapatali chifukwa ndi ofunikila kwambiri. Pamene amatifananiza ife ndi mchere , yesu akutiphunzitsa kuti tikhodza kukhala ofunikila ku dera lathu . Akutsimikiza kuti tikhoza komanso tikuyenera kukhala ngati mchere.

CHOCHITIKA MMAGULU AKULUAKULU (Gwiritsani ntchito **ZITHUNZI**: Sewero ” Sindingathe masamu”).

Zofunika : Ogulitsa mmodzi , ogula awiri , chimanga chogulitsa.

Chochitika : Ogulitsa akugulitsa chimangacho pa golosale pache. Ndipo ogula akubwera kuti adzagule chimangacho.

Ogula oyamba : *(akulowa mu golosalemo)* Tsiku labwino! Ndikufuna ndiguleko chimanga. Kodi mukupanga bwanji?.

Ogulitsa : Inde , Takulandilani.

(Ogulitsayo akupeleka chimangacho , Ogulayo akulipira , ndipo ogulitsayo akupeleka chenje kwa ogula oyamba uja).

Ogula Oyamba : *(Akutuluka ndipo ali panja akuwerenga chenje chakecho)* ! Akuti lero ndi tsiku langa labwino! Ogulitsa uja wandipatsa chenje chochuluka. Munthu osaphunzira chotani ameneyu, sadziwa ngakhale kuwerengetsa masamu! Hahaha!(kenako ogula oyamba uja akumapita).

Ogula wachiwiri : *(Akulowa mu golosalemo)* wawa!Ndabwera kudzagula chimanga.

(Ogulitsa akupeleka chimanga , ndipo ogula wachiwiri akulipira , kenaka ogulitsayo akupeleka chenje kwa ogula wachiwiriyo).

Ogula wachiwiri : *(Akupita kenako akuwerenga chenje chake)* akuti aah iyayi! Ogulitsa uja wandipatsa ndalama za chenje zochuluka . Wangolakwitsa ndipo akhoza kutaya ndalama zambiri kudzera mu njira imeneyi mu bizinesi yake.

Ogula wachiwiri : *(Akubwerela mu shopo)* Pepani . Ndalandila chenje chochuluka kwambir *(ndipo akubweza ndalama zoonjezerazo).*

Zikomo kwambiri , sindinamalize sukulu ndipo sindidziwa bwino kuonkhetsera . Izi zikundipangitsa vuto lalikulu ndi bizinesi yangayi . Ndinakakonda ndinakachita bwino mu masamu ine.

Ogula wachiwiri : Inde , ilidi ndi vuto. Mukudziwa , ngati mukufunitsitsadi kuphunzira , ine ndikhoza kukuphunzitsani kuti mwina bizinesi yanu ipite patsogolo.

Ogulitsa !- Zikomo kwambiri ! ndili okondwera chifukwa choti munabwera lero.

- Ndi uti mwa awiriwa amene anachita monga mmene khristu alili?. Ogula wachiwiri. .
- Ogula wachiwiri anali okhulupirika , ndi njira ina iti imene anachita ngati mkhristu?.
 - Anazipeleka ndi kuthandiza kuti ogulitsa adziwe masamu.
 - Anaona chosowa ndikuchita zinthu kuti zikhale bwino.

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Mu maphunzira a mbuyomu , tinaphunzira za mmene moyo wathu ukhoza ndinso mmene ukuyenera kuchitila ndi kukwezedwa ndi njira za Mulungu. Tsopano tikuona kuchokera ku zochitika izi komanso mmalemba kuti miyoyo yathu cholinga chake ndiko kubweretsa kusintha mdera lathu, mu mzinda wathu. Pamene mchere waikidwa , chakudya chimakhala bwino . Tikapita mu Madera athu , tikuyenera kupangitsa moyo wathu kukhala bwino wotizungulira.

Tonsefe timakhala mu Madera athuwo tsiku ndi tsiku chimene chikutipanga kukhala ndi mwayi kuti tikhoza kukhala ngati mchere mudera lathu. Zinthu zimene timapanga tsiku ndi tsiku mwina zitha kuoneka ngati ndi zosafunikila , koma monga mmene mchere umakhalira , umaoneka waung'ono koma ndi oti Utha kusintha chinthu chachikulu.

CHOCHITIKA CHA MMAGULU ANG'ONO ANG'ONO

Mu magulu a anhu atatu kapena 4 , yankhulanani zokhudzana ndi njira zomwe mumalumikizilana ndi anthu mdera lanu. Kodi mungakhale bwanji mchere pakati pawo- kupangitsa moyo wanu kukhala wabwino?

CHIONETSERO CHA MMAGULU AKULUAKULU

Malangizo kwa Mphunzitsi:Gwirani supuni yodzadza ndi mchere.

Funsani , kodi pali wina amene anakakonda kudya supuni yonse ya mchereyi?. (Ayi).

Zoona kuti 'ayi'! mchere umafunika kuti uzimwazidwa (onetserani powaza mchere mbale , mbeseni kapena pa tebulo)

Tikuyenera tonse tikumbukire choonadi chimenechi ngakhale ndi chophweka. Mchere nchito yake ndiyoti ukamwazidwe. Ngati tingobisala ndikumangoonetsera kumvera kwa Mulugu poonetsera ena ndi kuwakonda , ndiye kuti sitikuchita bwino. Taganiziani kumene mchere ukufunika!. Kodi umafunika mu zinthu zomwe zili ndi mchere kale wambiri?. (Ayi) Mchere wa moyo wathu ukuyenera kuti uzithandiza iwo amene alibe mcherewo pakadali pano. Makamaka kwa iwo amene mpakana pano samudziwa Yesu.

Ngati sitikupanga zinthu zabwino kwa ife komanso kwa anthu amene atizungulira. Ndyo kuti sitikukhala moyo wa khristu Yesu.

KUWALA

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Mulungu atalenga kumwamba ndi dziko la pansi , kuwala kunali chinthu choyambilila kulengedwa. Monga mmene sitingathe kukhalira pamene palibe mchere , sitingathenso kukhala pamene palibe kuwala. Kuwala ndikofunikira koposa pa moyo wathu.

- Kodi Kuwala kumachita chani?
 - *Kumapeleka moyo , kumaonetsa mtundu ndikukongola , kumaulula zoopsa zomwe zingathe kubwera.*
- Mungoyerekeza chikhala panalibe dzuwa , panalibe magetsi , panalibe mwezi . Kodi moyo unakakhala ngati chani?
 - *Palibe chomwe chinakakula pa dzikoli.*
 - *Sitinakaona , ngakhale sitepe imodzi patsogolo pathu.*

Werengani Yohane 8:12

- Kodi kuwala kwa dziko lapansi ndi ndani?
 - *Yesu*
- Kodi ndi chani chimene chimachitika pamene titsata yesu?
 - *Sitimayenda mu mdima , sitimakhala akhungu , tikhoza kuona komwe tikupita.*
 - *Tili ndi kuwala kwa moyo , tili moyo muzimu komanso tikukula.*

Yesu anati iye ndiye kuunika kwa dziko la pansi ndipo kuti tikhoza kukhala mmoyo umenewu pamene timutsata iye.

Werengani Mateyu 5:14-16.

- Kodi kuwala kwa dziko lapansi ndi ndani molingana ndi ndime imeneyi?
 - *Osatila ake- amene ndifeyo!.*
- Kodi Yesu akuti tichite chiyani kuti tikawalitse kuunikako?
 - *Zinthu zabwino.*
- Kodi kuwalako ndikwandani?
 - *Wina aliyense wa mnyumbamo , anhu onse.*
- Molingana ndi mau a Yesu ,kodi ndi chani chomwe chidzachitike pamene tiwalitsa kuwala kwa choonadi?
 - *Anthu ena adzaona ubwino wathu ndikutamanda atate wathu wakumwamba , kubweretsa ulemelero kwa Mulungu.*

Mulungu wapeleka mpingo(kapena akhristu ntchito yapaderadera: kuti akhale kuwala kwa dziko lapansi! Yesu anapeleka kuwala kwa chikondi chake kwa otsatira akewa. Opanda mpingo , palibenso kuwala kwina kulikonse, pamakhala chabe mdima okhaokha. Kumene anthu a Mulungu sanasankhe kupititsa kuwala .madera awo adzasala mu mdima. Opanda kuwala , palibe chiyembekezo mu ma dera athu.

NKHANI ZOKHUDZA MIPINGO YA KUUNIKA NDI MCHERE

CHOCHOTIKA CHA MMAGULU ANG'ONOANG'ONO

Malangizo kwa Mphunzitsi: Gawani gululi mmagulu atatu. Pakhale mtsogoleri mmodzi mu gulu lina lililonse. Gulu lililonse likuyenera kukhala ndikuwerenga nkhani zimenezi mu **bukhu la ophunzira** ndikuyankha mafunso. fotokozani kuti nkhani zonsezi ndi zokhudzana ndi midzi yeniyeni. Ndiye mulole gulu lina lililonse lipereke nkhani yawo ku gulu lonse.

DERA LOYAMBA : Mmudzi wina wake , pamene wina wake wadwala , asing'anga amabwera ndikudzawafunsa kuti athile nsembe ya nyama ndi cholinga choti alandile malangizo ndi mankhwala. A khristu a ku mpingo wa ku derail ataphunzitsidwa zokhudza ndi umoyo kudzera mu ndondomeko ya TCT , anayamba kugwiritsa ntchito maphunzirowa kumachiritsa matenda ena ndi ena mwa okha ndi ena omwe awazungulira . Anthu onse mmudzimu amatha kuona kuti anthu amene amatsatira malangizo awo amakhala bwinobwino opanda kupeleka nsembe ya nyama ayi. Ndiyeno , mudzi onse ukuyetsetsa kupewa matenda ndikumayesa kuchilitsa matendawa mwaokha kusiyana ndi kupeleka nsembe. Izi zikupulumutsa ndalama zawo ndikumakhalanso ndi thanzi! Zikuonetsa kuti kutumikila Mulungu kumapangitsa akhristu kukhala bwino . Kumapangisanso anthu ena kukhala bwino!.

DERA LACHIWIWI : Mmudzi wina , anthu amati akafika munthawi yokolola mmaminda mwawo , mwini wake wa mundawo amayenera apeleke zakudya zambiri ndizokumwa kapena mowa kwa anthu kuti anthuwa amuthandize kukolola. Nthawi zina , zomwe amaononga pa zakudya ndi zakumwazi zimapitirilanso phindu limene munthuyo wapeza ku kholola lakelo! Atatha kuwerenga ntchito zachikondi , akhristu mu derail anaganiza kuti azithandiza mmaminda a anthu osauka osafunapo malipiro a mtundu wina uliwonse, iwo sanangothandiza anthu a mu mpingo okha ayi komanso anathandizanso anthu ena amene ali akunja. Kenako anthu ena mderali anayamba kuona kuti zomwe anachita a khristuwa ndizabwino , nawonso anasiya kuitanitsa chakudya ndi zakumwa, pano wina aliyense wa mmudzimu akufunitsitsa kukagwira ntchito mmunda mwa ena kwa ulele. Wina aliyense amabweretsa zakudya zawo , ndipo amagwirila ntchito limodzi . Zotsatira zake ndi zakuti , banja lina lililonse likukwanitsa kupeza phindu. Tsopano nthawi yokolola ndi imene wina aliyense wa mmudzimu amaiyembekezera , poyamba anali kudandaula nthawi yokolola ikayandikila. Ndipo pano akumatha kudyetsa mabanja awo ndikusalanso ndi phindu.

DERA LA CHITATU : Mudzi wapanga chochitika chachikondi chomwe ndi mbali imodzi ya moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Amachita zimenezi sabata ndi sabata. Komanso , izi zakhala chikhalidwe chawo mu derail. Wina akaona chosowekera , amangosiya chomwe amapangacho ndikuyamba kuthana ndi vuto lija. Pakakhala miyala kapena zonyansa pamsewu , amaima ndikuchotsa zinthu zimenezi. Mudzi wawo poyamba unali onyasisitsa , opanda chitukuko mderali . Koma pano ndiwaukhondo komanso wachitukuko. Okha akwanitsa kumanga kachisi wabwino kudzera mu chuma chomwe achipeza mu kugwira ntchito molimbika ndi kuthandizana wina ndi nzake! Kusintha kukuonekera kwa wina aliyense amene akudutsa mmudzimu. Komanso zikuoneka mmene anthu a mmudzimo amakhalila wina ndi mzake . wina aliyense mderali ali okondwa ndikuthokoza kuti anthu a mu mpingo anawakonda koposa powaonetsa moyo wabwino oti azikhala.

- Kodi mpingo unachita chiyani mu nkhaninyi?.
- Kodi ndi kusintha kwanji komwe kunachitika mderali?.
- Kodi anthu a mu derali anachitapo chani?.
- Kodi akumauona bwanji mpingo?.
- Kodi tingakhale bwanji monga mpingo umenewu?.

KUPELEKA LIPOTI

Mulungu akufuna kuona Madera athu akuchiritsidwa . Kuchokera ku malemba amene tawerengawa ndi nkhani zomwe tawerengazinsu, tikuona kuti Madera athu chiyembekezo chawo cha machiritso amumpingo- dziko silingabweretse machilitso. Iye ndife kuunika kwa dziko lapansi kothamangitsa mdima mdera lathu!.

- Kodi mukhoza kunenako nkhani zina za ku dera lanulo zomwe zikuonetsera kuti kuwala kwa moyo ndikotani ndi mmene chawalitsilanso Madera athu?.
- Mmene ntchito ina iliyonse yachikondi yathandizila dera lanu.
- Kodi ntchito zanu zachikondi zafikila iwo amene ali kunja kwa mpingo?.
- Kodi ndi chani china chomwe mungamapange mdera lanu monga mpingo kuti mubweretse kuwala mdera lanu?.

MATHERO

Imani kuti muzifunse nokha: Kodi ndimakhulupirila ndithu pa chimene Mulungu amafuna cha anthu ake- kuphatikizapo ine ndi mpingo- kupangitsa kusinta mdera lathu?.

Pempherani kuti Mulungu atithandize kukhulupirira kuti iye akufuna agwire ntchito mwamphanvu kudzera mwa iye kukabweretsa kuwala kuchotsa mdima mmadera athu. Mufunсени Mulungu kuti akuonetseni njira imodzi ya mmene akanakugwiritsani ntchito monga kuunika ndi mchere , ndipo mumuyembekezere iye kuti akuyankheninso.

PHUNZIRO 2: KULEMEKEZA MULUNGU

Mfundo zenizeni:

1. Cholinga chokhalila mchere ndi kuunika ndi kuti tilemekeze Mulungu.
2. Tikuyenera kulemekeza Mulungu mu china chilichonse chomwe tikuchita.

ZIPANGIZO:

- Palibe

Chiyambi : Mulungu Olemekezeka ndi mtengo wake

Tisanapitilire , tiyeni tikumbukire zomwe tinaphunzira mu phunziro loyamba.

Werengani Mateyu 5:16 ‘Mwa njira yomweyo , lolani kuwala kwanu kuonekere pamaso pa anthu ena onse kuti akaone ntchito zanu zabwino ndikulemekeza atate wanu ali mmwamba.’

- **Kodi tikuyenera kuwalitsa kuwala kwathu chifukwa chani pochita zintchito zabwino kwa anthu ena?.**

Cholinga chakuchita zabwino-kukhala mchere ndi kuwala ndikuchita ntchito zabwino- ndi choti anthu ena akamulambile ndi kutamanda Mulungu! Timachita ntchito za chikondi chifukwa choti Mulungu akalemekezeke. Ndicho cholinga chenicheni chomwe tilinacho.

MIYOYO YATHU IKUYENERA KULEMEKEZA MULUNGU

KUKAMBIKANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Tiwerenga ndime kuchokera mu chipangano chakale lero. Mu ndime imeneyi , Ana a Isalaeri- Ana osankhika a Mulungu- anachoka ku ukapolo ku iguputo ku ukapolo ndipo amapita ku malo amene Mulungu anawalonjeza kudzera njira ya mu chipululu. Atafika kufupi ndi malo amene Mulungu anawalonjeza , anatuma akazitape kukalowa mzikomo , ndipo anaona kuti dzikoli linadzadza ndi zinthu zambiri zabwino- monga mikuku ya zipatso zabwinozabwino- ndipo kuti zinali zazikuluzikulu kuti zimafunika anthu awiri kugwirizana kuti anyamule. Koma anaona kuti panali vuto linalake- panali gulu la nkondo lalikulu kwambiri komanso anthu akenso a mphamvu kwambiri. Awiri mwa akazitapewa anapeleka uthenga wabwino wa zinthu zabwino , koma ena onsewo anapeleka zokhudzana ndi mavuto. Tatiyeni tiwerenge ku numeri chimene chinachitika.

Werengani Numeri 14:1-20.

Mu ndime imeneyi , anthu aku Isilaeri anachimwa . Mmalo moti amudalire Mulungu ndi malonjezano ake pa iwo, amadandaula za Mose komanso Mulungu , amanena kuti kunakakhala bwino chikhala anali akapolo monga mmene analili ku iguputo kapena kufera kusiyana ndi kufera mu chipululu (v.1-4). Poyankha , Mulungu akunena kuti adzaononga ana a Isaraeli ndipo adzapanga mtundu wa Mose. Mose akupita kwa Mulungu ndikumupempha kuti asanononge mtunduwu.

- Mu vesi 13-16 , kodi ndi chifukwa chiyani chomwe Mose akupeleka chomufunsira Mulungu kuti asachite chinthu chimenechi?
 - *Anthu ena adzamva za chinthu chimenechi nanena kuti Mulungu sakwanitsa kukwaniritsa malonjezo ake.*
- Kodi Mose akukhudzidwa ndi chani?
 - *Mbiri ya Mulungu , maka chimene anthu ambiri adzakhulupirile za Mulungu.*

Mose akukhudzidwa kuti ngati Mulungu ataononga ana a Isalaeri , ndiye kuti aiguputo adzanena kuti Mulungu sanakwanitse malonjezano ake ofikitsa ana a Isalaeri ku dziko lolonjezedwa. Mose akukhudzidwa ndi mbiri ya Mulungu- Ulemelelo wake! Akuganizila kuti , kodi “ kodi anthu osakhulupirila adzanena chani ngati chinthu ichi chingachitike?” Mose sakunena kuti , “ Musationonge chifukwa ndife anthu abwino ,ayi! , Kapena kuti mwina izi zidzandipangitsa kukhala mtsogoleri osauka. ” Chomwe chikumukhudza kwambiri Mose ndi mbiri ya Mulungu.

- Kodi inu mumaganizirako za mbiri ya Mulungu?.
- Kodi ife monga a khristu , tikuyeneranso kumaganizila za mbiri ya Mulungu(kapena ulemelero wake?) ndi chifukwa chiyani mukutero?.

Werengani 1 Akorinto 10:31.

- Molingana ndi Paulo , kodi ndi pati pamene tikuyenera kukhudzidwa ndi ulemelero wa Mulungu?.
 - *Paliponse pamene tikuchita chinthu china chilichonse- ngakhale chophweka ,, ntchito zazing’onozing’ono kudy a kapena kumwa.*
- Ngati manyumba a akhristu samasamalidwa bwino mdera , katundu wawo sakusamalidwa , ndipo ana awo amaoneka opanda ukhondo , kodi mukuganiza ngati anthu a mdera lanu aziganiza bwanji za Mulungu wanu?.
 - *Akhodza kudabwa ngati Mulungu amasamalira anthu ake , atha kuyamba kukhulupirila kuti Mulungu amangosamalira chabe zinthu za uzimu wa anthu koma sasamala za mabanja awo.*
- Kodi zikutanthauza kuti tikhale olemela kapena angwiro kuti tilemekeze Mulungu cholinga choti anthu atisilile?.
 - *Ayi! Makamaka!, Yesu mwini wakeyo anabadwilanso mu banja limene ndi losauka. Komabe , tikuyenera kupanga chothekeracho pa zochepa zimene Mulungu watipatsa . Tikuyenera kugwiritsa ntchito zipangizo zomwe tili nazo ndi maluso onse amene tili nawo kuti tibweretse ulemelero wa Mulungu!.*

Taitanidwa kuti tikabweretse ulemelero kwa Mulungu mu zinthu zonse zomwe tikuchita. Iyi ndi nkhani ya mmene izi zikhodza kuchitira.

Panali banja lina limene linasamutsidwa kupita kudera lina kukakhala mu malo osungilamo anthu amene avutika ndi nkondo mu dzikolo. Nkhondo isanayambe , banjali linali lachuma. Tsopano achoka , asiya kukhala pabwino , pano akukhala mkachisasa. Mzimayiyu sanasamalire kanyumbako ndipo pang’onopang’ono kanaonongeka. Iye anasiya nyumba yokongola imene anakonda kukhala ndi kuganizira zinthu zimene iye analibe. Anasowa mnyumba yabwino imene amkakonda kumakhala kwawo ndipo amangoganizila chinthu chimene iwo analibe. Pakupita kanthawi , mlamu ake wamamuna wamkulu anabwera kudzakhalala ndi iye. Anasamalira nyumbayo komanso dera lonse , naikonzanso nyumbayo , ndipo anatenga maluwa ndikuyesesa kuti abweretse ulemelero wa Mulungu panyumbapo. Anakhala masabata awiri akumapanga zinthu zimenezi opanda kugwiritsa ntchito ndalama ina iliyonse. Pophatikiza zomera ndi maluwa ndikuonetsetsa kuti nyumba ili mwa ukhondo , komanso yosabalalika , mmene anthu anayamba kumvera zinasiyana. Izi zinapeleka chiyembekezo osangoti chabe kwa mulamwakeyo , komanso kwa anthu m’banjali ndi anthu a mderali. Ngakhale banjali linakalibe losauka koma nyumba inalinsu yaing’ono komanso yonyozeka , mbale wawo uja anagwiritsa ntchito zomwe anali nazo kupeleka ulemelero kwa Mulungu mu nthawi ya masautso.

CHOCHITIKA MMAGULU ANG’ONOANG’ONO

Mmagulu ang’ono ang’ono, tulutsani ziganizo zochulukilapo za mafunso awa ali mmusiwa.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Ngati mkofunikira, yambani ndikutulutsa mfundo zochepa limodzi cholinga choti amvetsetse kuti kodi ndi mayankho a mtundu wanji amene akufunika. Pamene magulu amalizitsa, aloleni tsopano anene chomwe akambirana.

Kodi ndi njira zina ziti zomwe tingakonzere mbiri ya Mulungu pakati pa akhristu?.	Kodi ndi njira zina ziti zomwe tingaonongere mbiri ya Mulungu pakati pa akhristu?.
<ul style="list-style-type: none"> • Kusamalira ana athu. • Kukonda akazi athu. • Kulimbikila. • Kutumikila ena. • Kutsatira ndondomeko zabwino za umoyo. • Kuyang'anila chilengedwe, nyama, ziweto. • Kusamalira zipangizo zathu bwino. 	<ul style="list-style-type: none"> • Kusasamala ma banja athu. • Kuononga chilengedwe. • Kusasamala matupi athu (kusuta fodya, kuledzera). • Kukwiya. • Kusakhulupirika muzochitika za tsiku ndi tsiku. • Kusakhala okhulupirika kwa okondedwa athu. • Kumenya ana athu, abwenzi athu, ziweto.

PELEKANI LIPOTI

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

- Anthu akayang'ana moyo wanu, kodi amaganiza kuti Mulungu ndiodabwitsa. Malamulo ake ndi abwino! Njira zake ndizapamwamba!. Kodi kapena amaganiza kuti Mulungu wathu siwamphamvu kapena osafunikila?.
- Kodi tikumunvera Mulungu mu dera lina lililonse la moyo wathu?. Kodi tinakhala ndi anthu ena mwa ulemu?, kodi ndalama zathu timazisamalira?. Kodi ndife okhulupirika?. Kodi timapeleka molowamanja?. Kodi ndi chani chomwe tingachite chosiyana ndi ena?.

AKAZEMBE A MULUNGU

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Mbiri ya Mulungu ndi yofunika kwambiri. Watitcha ifeyo monga akazembe.

Werengani 2 Akorinto 5:20.

- Kodi kazembe ndi ndani?.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Chotsani maiko ndi kuikaponso maiko amene ali odziwika bwino kwa anthu amene mukuwaphunzitsa?.

Kazembe ndi amene amachoka ku dziko la kwawo kupita ku dziko lina kukaimilira dziko lake. Mwa chitsanzo, Ku Malawi kuli kazembe wa ku South Africa. Iye amaimila south Africa mu Malawi. Ngati boma la south Africa lapanga chiganizo china chilichonse, kazembe ndi amene amalankhula mmalo mwa dziko lake. Amauza anthu a ku Malawi za chikhalidwe cha anthu a mtundu wake ku south Africa. Amawalimbikitsa kuti adzapiteko ku South Africa, amayambitsa ma bizinesi ku Malawi ndipo amagulaniso zinthu za ku Malawi komweko. Amaimililanso South Africa potenga nawo mbali pa zochitika ndikumaonekera pamaso pa anthu—chilichonse chomwe amachita ndi chomwe amavala, cholinga chake ndi choti chikabweretse ulemu kupindulira dziko lake.

Ifenso ndife akazembe, koma mu ufumu wakumwamba, pamene anthu akutiona ife ndi moyo wathu wa tsiku ndi tsiku, akuyenera aone chimene ufumu wa Mulungu ulili.

- Kodi miyoyo yathu imauza chani anthu za chimene ufumu wa Mulungu ulili?.

Taganizani mmene mwamuimilila Mulungu mu sabata yomwe yangothayi. Kodi anthu akakuonani mmoyo wanu, kodi ndi chani chimene angamvetsetse cha Mulungu?.

Mmagulu , ganizilani zinthu zina zapadera zomwe mukuyenera kuchita sabata imeneyi.Pempherani limodzi kuti Mulungu akuthandizeni kubweretsa kusintha kumene mukufunako.

Kukhala pa ulemerele wa Mulungu kutha kutidzadza ndi chimwemwe mu nyengo zonse.

1 Petro 2:12, Imati , " Mukhale moyo wabwinowo pakati pa iwo amene sakhulupirila , kuti ngakhale akuweruzani pa ntchito zoipa , akhoza kuona ntchito zanu zabwino ndikulemekeza Mulungu pa tsiku limene adzabwera.

11

PHUNZIRO 3 : CHI KHRISTU CHENI CHENI

Mfundo zenizeni:

1. Chi khristu chenicheni chimachokera ku chimene tili mkati mwathu , osati zochitika za kunja kwathu ayi . zochitika izi zikuyenera kukhala zotsatila za chikondi chathu kwa Mulungu.

ZIPANGIZO: :

- ZITHUNZI: 3 KHADI Yoonoetsa malangizo a kaseweredwe.
- Ma kandulo ndi machesi atatu (mukafuna).

CHIAMBI

KUKAMBILANA KWA MMAGULU ANG'ONO ANG'ONO

- Kodi mungamufotokoze bwanji mkhristu weniweni? Kodi mungamuzindikile bwanji mkhristu weniweni? Pangani mndandanda wa zinthu zomwe amapanga kapena khalidwe la moyo wawo.

KUPELEKA LIPOTI

Malangizo kwa Mphunzitsi: Lolani maguluwa apeleke zizindikilo zomwe analemba zija. Kenako , funsani gulu lonse kuti aunikile mndandanda wawo . Kodi ndi zinthu zingati zomwe zili pa mndandandapo . Kodi ndi zinthu zingati zomwe zili pa mndandandapo koma zili zochitika monga kupita ku kachisi?. Kodi ndi zingati zomwe zili zachikhalidwe cha munthu monga kukhulupirika?. Kodi ndi mndandanda uti omwe uli waukulu?.

Lero tinaona zisanzo zitatu za chikhalidwe cha chikhristu.

KHALIDWE LOYAMBA: KUNJA KOKHA BASI

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU: SEWERO

Malangizo kwa Mphunzitsi: Muzafunika anthu atatu ozipeleka . Pamene Mukupereka ma khadi a **ZITHUNZI** kuti anthu apangile sewero , onetsetsani kuti ozipelekawo ali okonzeka kuchita kutsatila njira izi!.

- Khalidwe loyamba , azichita monyada.
- Khalidwe lachiwiri –oweruza ndiponso ozuzula.
- Khalidwe lachitatu , ozichepetsa ndipo olapa.

KHALIDWE LOYAMBA : (ACHITE MONYADILA).

Ow! Mmene ndalalikila lero mosangalatsa ku khwimbi la wanthu mu mzinda onse. Ma sipika anga mmene analili othandiza ka wina aliyense kuti azimva kuchokera pamene alipo kuti azimva mapemphero anga ofunikila aja ndi malamulo okhudzana ndi za uzimu!. Ndinawauza njira zonse zomwe akuyenera kuyenda . Ndikuziwa ndinakopa mtima , chifukwa wina aliyense anakweza manja ake kuti akhale tsopano a khristu pamene ndinamaliza kulalikila. Inedi ndithu ndine mlaliki wamphamvu kwambiri mu dera lino- palibenso wina amene ali ndi chipambano ngati chomwe ndikuchitila! Sizikudabwitsa: ndimatha maola awiri ndikupemphera , ola limodzi kuwerenga Baibulo tsiku ndi tsiku. Monga sabata yatha ndinasala kudya ndipo ndimamufunsa kuti atembenuze anthu 150 pa mwezi. Ndikutsimikiza kuti akaona mmene ndimasalira kudya ndi kupemphera , ndiye kuti atiyankha basi. Ndizoipa kuti anthu ena Sali auzimu monga mmene ine ndilili. Sakuziwa konse mmene ndilili ine ozipeleka ku ntchito ya Mulungu.... ooh! Komanso pali mkosana uja ndayandikana naye koma amaledzera kwambiri. Zikuonekanso ngati sakhoza kuona njira yopitira kwawonso koma yakwana kale 5 koloko ! iyeyu akuyenera kumvako za ma selemone anga basi! Chabwino , koma ndiliba kaye nthawi ya munthu ameneyu pakadali panopa ndilibenso nthawi ya munthu ameneyu konse ayi!. Ndi nthawi yopemphera tsopano- (lye akuthamanga kumapita).

- Kodi mungafotokoze bwnaji khalidwe la munthu oyambayu?
 - *Akungokhudzidwa ndi zinthu za ulemelero wake okha , palibepo zinthu za uzimu , palibenso ntchito za chikondi.*
- Kodi munakumanapo ndi munthu wina wake ngati ameneyu?.

Munthu oyambirila uja ali ngati mfalisi . afalisi anali atsogoleri a mpingo mu nthawi ya Yesu . Amapeleka nthawi yawo yonse kuwerenga ndi kuphunzitsa malamulo a Mose. Amakhudzidwa kwambiri ndi kutsatira malamulo a Mulungu ndikukhala molungama. Kufikila pokuti anaonjezeranso zinthu zoletsedwa 365 ndi malamulo ena 250 kuphatikiza pa malamulo 10 omwe analipo kale aja amene tinakafuna wina aliyese kuti aziwasatira. Afalisi amaonedwa kuti anali anthu achiyero kwambiri kuposa anthu ena onse. Munthu wamba sanakayerekeza kukhala monga mmene iwo analilimu.

Komabe , kawiri kawiri mu baibulo tikuona kuti Yesu amawadzudzula afalisi samene amawengedwa ngati anthu olungama kwambiriwa , komanso, Yesu amakonda kulankhula mau ankhanza osati kwa mahule ayi koma kwa afalisi , tawerengani chomwe iye analankhulacho.

Tawengani mateyu 23:1-7 , 23-28.

- Ma vesi amenewa , kodi mukuganiza kuti tchimo la afalisi linali lotani?
 - *A falisi anali ndi zochitika zonse zolondola , koma mkati mwawo munali mkhwidzi , kunyada , amangosangalatsidwa ndi za iwo okha , ndi kuzikweza okha. **Samasamala za anthu ena** koma amaika milingo yolakwika ndi kulamula zinthu zosayenera . anthu amalephera kukwaniritsa zinthu zimene a falisi amalamulira . komanso iwo sanali olungama . **amayetsa kuzionetsa ngati ndi olungama ndipo amaweruzwa mosayenera konse. Afalisi samakhudzidwa ndi za kukhala moyo wa chiyero mmene amaonekera kunja kwawo kuti anali achiyero.***

Pamene Mfalisi ndi khalidwe lake mu sewero lathu loyamba lija ndiye chitsanzo cha anthu amene aja , tonsefe tikhodza kuyesedwa kuyerekeza ngati tili auzimu kwambiri kuposa mmene tilili , ndithu monga mkhristu pamene tikumva kutalikana kwakukulu ndi Mulungu, Mulungu sakusangalatsidwa konse ndi mmene timazonetserera kunjaku ngati tili pamaso pake. Ntchito zathu zakunja zikuyenera kuchokera ku ubale oyandikana kwambiri ndi Mulungu.

Tsopano , tatiyeni tione khalidwe lina lotsatira.

Khalidwe lachiwiri: Kutumikila opanda chikondi

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU: SEWERO

Malangizo kwa Mphunzitsi: Gwiritsani ntchito makhadi a **ZITHUNZI**.

Khalidwe lachiwiri: (Amachita ngati akunyansidwa, ndikuganiza mokhumudwa, ndikukhala okwiya pamene akulankhula.) Huu! Tsiku lotani ili , ndatopaaa ! kukhala mbali imodzi ya mpingo kukundithera nthawi yanga yambiri! Sabata ina iliyonse ndimatenda nthawi yanga kuthandiza anthu ena.ndichifukwa chake abusa anandiuza kuti ndine mdalitso waukulu kwambiri ku mpingo! Lero lomwe , ndayendera anthu atatu odwala ndipo ndinawabweretsera chakudya. Sabata yomwe yangothayi , ndinakonzanso kumangidwa kwa nyumba ya mkazi wamasayiye... (ndipo amayamba kukwiya) osati ndikumumvetsetsa mzimayi uja ayi. Koma akuoneka kuti sanali othokoza, sananene kuti zikomo , koma anakhalanso ngati akungotenga ngati anayenera kulandila zinthuzi. Sindimakonda anthu angati amene aja. Samamvetsetsa kuti ndimapeleka nsembe yochuluka bwanji kuti ndiwathandize. Ndimasiya banja langa cholinga ndikawathandize anthu amene aja. Koma ndithu analibe kuthokoza. Anthu akuyenera kulemekeza zomwe ndikuchita. Mzimayi opusa , ndinakakonda ndisamuthandizenso komwe.

- Kodi mungafotkoze bwanji khalidwe la munthu wachiwiriyu?
 - *Kugwirila ntchito limodzi pa zochitika za pa mpingo koma ndi zolinga zolakwika.*

Chikhalidwe china ndikhudzana ndi mbiri yake. Amachita ntchito zachikondi koma ndi zolinga zolakwika. Cholinga choti anthu ena amutamande . tatiyeni tione ndime ina yokhudzana ndi vutoli.

Werengani 1 akorinto 13:1-3.

- Kuchokera ku malemba amenewa , kodi ndi chani chomwe chimasowekera mu khalidwe lachiwiri lija?. (Chikondi)

Baibulo likutiiza ndi kutiphunzitsa za kutumikila anthu ena opanda chikondi mmitima mwathu ndi zosakwanila ayi! Tikumvetsetsa kuchokera mu ndime imeneyi kuti tikuyenera kukhala ndi chikondi kuti ife tichite bwino ntchito za chikondizo.

KUKAMBILANA KWA MMAGULU ANG'ONO ANG'ONO

Tangoyerekezani munthu wachiwiri uja atabwera kwa inu kuzafuna madalitso. Anamva za ulaliki okhudzana ndi 1 akorinto 13 koma samamvabe zakukonda wena. Amafuna kukonda koma amaganizila kuti nanga azikonda bwanji anthu ena mwa anthuwo? Makamaka kwa ena mwa iwo amene anali okhumudwitsa . Kodi ndi malangizo anji amene mungapeleke kwa munthu wachiwiri zokhudzana ndi mmene tingakuzile chikondi chatu pa anthu ena?.

KUPELEKA LIPOTI

KOMWE CHIKONDI CHICHOKERA

Ngati tifukufuna tikule mu chikondi , tikuyenera tikaone kaye pamene chikondicho chinayambila.

Werengani 1 Yohane 4:7–9.

Kodi chikondi chimachokera kuti? Chikondi chimachokera kwa Mulungu. Mulungu ndiye chikondi.

Chifukwa choti chikondi chimachokera kwa Mulungu , tikuyenera kuyangana kwa Mulungu kuti atipatse chikondi chochuluka pamene sitikumva ngati kukondedwa.

CHIONETSERO CHA MMAGULU AKULUAKULU (MUKAFUNA)

Malangizo kwa Mphunzitsi: *Sankhani mmodzi ozipeleka kuti abwere kutsogolo . Mupatseni kandulo osayaka.*

Mulangizeni munthuyo kuti ayase kanduloyo . (Ndi zosatheka kuti ayase kanduloyo opanda moto.

Funsani:

- Kodi simukuyatsa kanduloyo chifukwa chani?
 - *Chifukwa ndilibe moto/ machesi.*
- Kodi mukufuna chiyani?
 - *Moto/ Machesi.*

Malangizo kwa Mphunzitsi: *Funsani ozipelekayo kuti apitililebe kukhala kutsogolo. Mpateninso kandulo wina osayakanso munthu wina. (Izi sizithekabe chifukwa padakalibele moto/macheso).*

Funsani.

- Kodi simukuyatsa kandulo wa mzanuyo bwanji?. Chifukwa nanenso kandulo wanga ndi osayatsa.
- Sizipeleka tanthauzo kumayesera kuyatsa kandulo wa munthu wina wake pamene mulibe kuwala kwa inu mwini?. Ayi sichoncho!.

Monga mmene sitingayatsire kandulo opanda moto kapena macheso , sitingadzadzidwe ndi chikondi pamene palibepo choyambitsa chikondicho.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Pa tebulo yomwe ili patsogolo pa chipindacho , yatsani kandulo wamkulu.

- Nenani kuti , “ Yesu ndiye kuwala kwa dziko lapansi. Chiyambi cha kuwala kwathu kumachokera kwa Mulungu kudzera mwa Yesu khristu.
- Funsani ozipeleka wachiwiri, “ Kodi mutabwera ku kuwala kumeneku , kodi mungathe kuyasa kandulo wanu?. (Inde).
- Nenani kuti “ Tsopano mwadzadzidwa ndi kuwala chifukwa inu mumafuna kuwalako . tsopano mungathenso kuyatsa kandulo wa amzanuwo?. (inde).
- Langizani oziperekayo kuti ayatsenso kandulo winayo.
- Kodi tikuphunziramo chiyani mu chionetsero chimenechi?
 - Yesu ndi kuwala komanso chiyambi cha chikondi chathu. Sitingaonetsere chikondi bwinobwino opanda chikondi chake.

Ndi zomvekeratu bwino kuti tikuyenera kupita kumene chikondi chimayambira ndi cholinga kuti tikule mu chikondi ndi cholinga choti tikawaonetse anthu ena chikondi cha khristu.

KUKULA MU CHIKONDI

Mmmene tinatchulira kuti tikhoza kukula mu chikondi pamene tikupemphera ndi kumufunsa Mulungu kuti aonjezere chikondi chathu. Izi ndi ziganizo zinanso.

1. PEMPHERERANI ENA.

- Chikondi chimakula pamene tikupempherera anthu ena- ngakhale iwo amene samatikonda ayi. Mufunsemi Mulungu kuti akupatseni chikondi cha pa iwo. Pamene mukupititsa nthawi kumawapempherera tsiku ndi tsiku. Muzadabwitsidwa kuti Mulungu adzasinthile kaganizidwe kathu pa iwo. Izi zimatenga nthawi!.

2. CHITANI/ MVERANI.

- Chikondi chimakula pamene tikuchita; chikondi si chimene mumangochimva chabe ayi. Nthawi zina ndi choyenera kuchitika ndithu. Choncho ngakhale sitikuganizila zomukonda wina wake , tikhodza kuyeserabe kuonetsera chikondi kwa wina wake ndikupemphera kuti chidwi chomukonda chikule mwa inu.

3. TENGANI NTHAWI YOPHUNZIRA ZA ANTHU ENA.

- Kawirikawiri , ngati tiphunzira za anthu ena , chikondi chathu pa iwo chimakulakula.

Sungani ichi mmalingaliro: kukonda wina wake sizikutanthauza kuti mukugwirizana ndi zonse zomwe mumachita. Ngati wina akuchimwa , ife sitigwirizana ndi tchimolo, koma timawakonda ochimwawo. Yesu amakonda kukhala ndi mahule ndi otolela misonkho , iye anawakonda anthuwa , amadya nawo , amagawana moyo wake ndi iwo ndikuwapulumutsa kudzera mu chikondi chake pa iwo.

KHALIDWE LACHITATU : KUTUMIKIRA NDI MTIMA ODZADZA NDI CHIKONDI.

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU:

Malangizo kwa Mphunzitsi: Gwiritsani ntchito ma khadi a **ZITHUNZI**.

KHALIDWE 3 : (AMACHITA MOZICHEPETA NDI MOLAPA).

Ndinasangalatsidwa ndi chitsanzo choyamba ndi chachiwiri . anthuwa ndi a uzimu ndipo akuchita zinthu zambiri zabwino pa mpingo. Koma zikuonetsa ngati sindingakwanitse kukhala wabwino mmene iwo alili lero.

Ndinali ndi nthawi yaitali kupemphera, koma patangotha mphindi zochepe , mwana wanga anagwa ndikuvulala pa bondo , ndiye ndinasiya kaye kusamalira mbalezo kuti ndimumange pabalapo. Kenako inakwananso nthawi yoti ndimutengele mwanayo ku sukulu. Kenako , kenako ndinapita ku munda kukagwira ntchito , mmene ndikubwerela kuchokera ku mundako , ndinaima kuti ndimuyendere mzimayi wina wa masiye. Mzimayi osauka- amene wangotaya mamuna wake cha posachedwapa , ndipo mtima wake ndi osweka. Ndikumumvera chisoni kwambiri. Tinakhala ma ola angapo tikulankhulana , pamene ndimawathandiza ndi zinthu zina monga kuchapa , ndiponso ndinapemphera nawo. Anali okondwa kwambiri , koma ine ndinakakonda panakakhala zambiri zomwe ndinakachita pomuthandiza munthuyu. Mtima wanga wasweka , mbuye ndikhululukilani pa njira zomwe sindili olungama. Ndikufuna ndikhale moyo umene umakusangalatsani inu nthawi zonse.

Ndionetseni mmene ndingapangile ndi nthawi yanga kutinso ndingakonde anthu ena motani. Ndithandizeni chifukwa sindingathe pandekha.

- Kodi mungafotokoze bwnaji khalidwe lachitatu?
 - *Ozichepetsa , osamalira , kuonetsa chikondi ndi mbali imodzi ya moyo wa tsiku ndi tsiku. Iyeyu ndiye mchere weniweni ndi kuunika.*
- Kodi nthawi yake anapanga nayo chani?. Amachita ntchito zachikondi , kukhumba kuononga nthawi yake mu pemphero.
- Kodi mukudziwa bwanji kuti mkaziyu anali ndi mtima odzadza ndi chikondi?. Amanva chisoni ndi mzake , amafunanso ulemelero wa Mulungu.

KUKAMBILANA KWA MMAGULU ANG'ONO ANG'ONO

Welengani Luka. 18:9-14.

- Kodi ndi ndani amene Mulungu anamuyamikila mu ndime imeneyi?.
- Kodi ndi chani chomwe chilli chodabwitsa pa nkhanayi ? kumbukilani chomwe tinaphunzira chokhudzana ndi afalisi?.
- Kodi ndi sewero liti mwa atatatuwa lomwe mukuganiza ngati ndilimene likufotokoza mtundu wa akhristu amene Mulungu akufuna?.
- Kuyang'ananso tanthauza lanu lenileni la mkhristu weniweni . Kodi mungakokere motani mutapatsidwa mutaona zomwe zachitika mu phunziroli tsopano?.

Khalidwe lachitatu amenena molingana ndi mmene iyeyo alili , kuchita ntchito zake tsiku ndi tsiku ndi mtima wake onse kukhumba ulemelero wa Mulungu. Analibe maphunziro ena apadera ndipo samaimanso monga wina wake amene ali wapaderadera kwambiri. Koma anali ndi mtima wachikondi ndi mtima umene wakonzekera kugwira ntchito mwa chikondi . amachita ndi chifundo ndipo amamufuna Mulungu mu mapemphero. Anali okhulupirika ku ntchito zake za tsiku ndi tsiku komanso amapanga zachifundo pa antu amene amuzungulira. Khalidwe lachitatuli likuonetsera kuti sitikuyenera kukhala olungama kuti timutumikile Mulungu! Mulungu amafuna kuti tizimupatsa chomwe ife tilinacho(moyo wathu watsiku ndi tsiku) ku ulemelero wake.

Kutumikila ena ndi mtima odzadza ndi chikondi ndi chimene chimabweretsa Ulemelero kwa Mulungu ndipo zimapangitsa anthu ena kuti azimutamanda iye!. Njira yokhayo yokhala ndi mtima odzadza ndi chikondi ndiko kukhala kufuna Mulungu mmalo mwa ife eni ake.

MATHERO

Mu maphunziro athu awiri apitawo , taphunzira kuti zochitika zambiri za akhristu – timayenera kukhala mchere ndi kuunika, ndipo tikatero tibweretsa ulemelero kwa Mulungu. Zimayamba ndi ubwenzi wabwino ndi

Mulungu. Opanda chimenechi tizakhala ngati magulu awiri oyambilira aja- mwina kuchita zinthu muli kutali ndi Mulungu kapena kutumikila koma kusowa chikondi ndikukhala ozikweza.

KUUNIKILA PANOKHA

Taganizilaninso zikhalidwe zomwe ziili mu sewero lija- kodi inu mukufanana ndi uti? Mufunseni Mulungu kuti akuyezeni mtima wanu ndikukuonetsani mayankho ku mafunso ali mmusiwa:-

- Kodi ndikufuna kulandila ulemelero ndi matamando chifukwa cha chimene ndimachita? Kapena ndili kwambiri kukhudzidwa ndi anthu kuti azindilambila ine?.
- Ndikufunafuna Mulungu mwa choonadi , kapena ndikungochita chinthu choyenera , kapena ndikungochita chithu choyenera kunja kokha basi? Njira imodzi yodziwa ndiko kuona munthu amene muli ngakhale palibe wina aliyense amene akukuyang'anirani?. Kodi muli otanganidwa motani pamene muchita zinthu pomwepalibe wina amene akukuyang'anani?. Kodi inu mumakonda ndithu kapena muli achidwi ndi anthu kumakuganizilani kuti ndinu oyera?.
- Ndimatha kukonda anzanga , kapena ndikufuna ndichite kumufunsa Mulungu kuti andisinthe mtima wanga kuti ndikakhale ndi chikondi chenicheni?.

Pempherani panokha , kapena awiri awiri , kapena ngati gulu kuti Mulungu asinthe mitima yathu ndipo kuti zochitika zathu zikaonetsere kuwala kwa chikondi chatu ku Madera athu.

Ma phunziro athu otsatira azatiphunzitsa kuti kodi tikule bwanji mu uzimu cholinga choti mitima yathu ikapangidwe yosangalatsa Mulungu.

PHUNZIRO 4: KUCHOTSA TCHIMO

NDIKUKONZANSO MALINGALIRO ATHU

MFUNDO YENIYENI:

Tikuyenera kutengapo gawo ndi kugonjetsa tchimo ndi cholinga chogonjetsa tchimo ndikuti tikhale ngati kuunika ndi mchere mu Madera athu.

ZIPANGIZO:

- Bukhu la ophunzira: ma sitepe ogonjetsera(ndi malemba komanso zithunzi).
- ZITHUNZI: Sewero la Ma Dontho akuda(Black dot) (sindikani ma khadi okwanila kuti wina aliyense akhale nayo yake- dulani mndandanda oyamba kuonetsa gulu ndikudula gawo lotsatiralo padera ndikuika mu univolopi kapena chikwama).
- ZITHUNZI: Zithunzi sikisi- zitatu za ma sitepe okhudzana ndi " Kuchotsa tchimo , ndipo enawo okhudzana ndi kukonzanso malingaliro athu".
- Ma sitepe 9 akugonyetsa tchimo (positala) (konzani izi pa bolodi yoyera) pakhale mpata kapati pa sitepe ina iliyonse.

Malangizo kwa Mphunzitsi: *Ndi chinthu chofunikila kuyesera zionetsero za phunziro limeneli musanazifikitse kwa anthu kuti muonetsetse kuti mfundo imeneyi izafikitsidwa pa malo ake oyenera ndikuti wina aliyense azakhodza kutolapo kanthu. Komanso sewero la gulu lalikulu. Ndikwabwino kukhalilatu ndi zipangizo zonse zofunikila nthawi isanakwane..*

CHIYAMBI: Kutaya mchere wathu

Mu Phunziro 1 , tinawerenga mateyu 5:13 , ' Inu ndi mchere wadziko lapansi , ungakhalenso bwanji ndi kukoma kwake? Umakhala opanda ntchito . kuti ukangotaidwa ndikumapondedwa ndi anthu.

T inalankhula za kufunika kwa mchere ndi mmene moyo wathu ukuyenera kufananila ndi mchere mu zochitika zathu mu dera lathunso. Tsopano tiona gawo lachiwiri la ndime imeneyi- kodi ndi chani chomwe chimachitika mcherewo ukachoka mphanvu yake?.

Kuchotsa Tchimo

- Kodi tchimo ndi chani?. (Kuchita zolakwika , maganizo oipa kapena zochitika zolakwika ndi kumulakwilanso Mulungu).
- Kodi zitanthauzani kukhala ochimwa , (tikufuna kuchimwa , tili ndi chikhalidwe chochimwa ,Tili ndi uchimo miyoyo yathu).

Tchimo limatipangitsa kukhala opanda mchere ndiosapindula mu dera lathu. Tisewera sewero lophweka kuti tipeze kuti ndi ndani mwa ife amene tikuyenera kugonjetsa tchimo miyoyo yathu.

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU: SEWERO LA MA DONTHO AKUDA.

Malangizo kwa Mphunzitsi: *Onetsani gulu **ZITHUNZI**: Ina yokhala ndi dontho limodzi lopanda kanthu ndi lina lokhala ndi kudetsa.*

Dontho lopanda kanthu limaonetsera mtima oyera umene ulibe uchimo ndipo dontho linalo limene likuoneka ndi kudetsalo limaimilira mtima okhala ndi uchimo.

CHochitika chimenechi , tigwiritsa ntchito kutsogolo kwa chipinda. Malo Awa agawidwa Madera awiri.


- Dera loyamba- “ La uchimo’ .’
- Dera Lachiwiri- “ La osachimwa”



MALANGIZO A SEWEROLI.

1. Wina Aliyense wa
2. Wina aliyense wa inu azalandila khadi ya dontho. Azaona kuti ndi mbali iti ya chipindamo yomwe azayenera kulowera. Ma dontho akuda=’dera la uchimo” kapena dontho yosadetsedwa=dera la osachimwa.
3. Musayang’ane pa dontholi kufikila pamene ndikulangizeni kuti ndi nthawi yanu. Sunganibe khadi yanu kuti pasakhale wina amene aone dontho lanu- ngakhale mwini wake inu!.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Aonetseni khadi ya **ZITHUNZI** yomwe ili ndi ma dontho akuda ndikuonetsera kuti khadi imeneyi ndi imene ingawapangitse kutipa ku mbali ina ya chipindacho imene yaikidwa kuti ndi ya anthu ochimwa okhawa “ onetseani khadi imene ili ndi dontho losaika kalikonse ndikuonetseranso kuti khadi imeneyi ingawatumize ku mbali ina yomwe yaikidwa kuti ndi ya anthu osachimwa.



- Pelekani khadi imodzi pa munthu wina aliyense (gwiritsani ntchito ma dontho akudawo).
- Muwakumbutse kuti asayang’ane pa khadi lawo.
- Mmodzi mmodzi funsani kuti azibwera kutsogolo ndipo aziyang’ana khadi yawo ndipo azionetsa ku kalasi yonse.
- Alangizeni kuti apite ku mbali yoyenera molingana ndi zomwe apeza pa khadi lawo ndipo apitilire kugwira khadi lawo moonetsera kuti gulu lonse kuti kalasi yonse ithe kuoneka bwino.
- Pamene wina aliyense watenga mbali yake , otenga nawo mbali onse azikhala ku chipinda chomwe chalembedwa kuti “ Ochimwa”.
- Ndiye werengani zinthu izi.

Monngana ndi 1 Yohane 1:8 , tonsefe tinachimwa , ‘ ngati tinena kuti tilibe uchimo , tizinyenga tokha ndipo choonadicho sichili mwa ife.” Chifukwa choti tonse tinachimwa , tonse tikuyenera kudziwa za mmene tingachotsere uchimo kuti tipangidwe kukhalanso mchere.

KUUNIKILA PA WEKHA NDI PEMPHERO.

Tiyeni titengepo nthawi kupemphera tidakali chiimile . Muthokozeni Mulungu chifukwa cha malonjezano ake otikhululukila ndikutipatsa mitima yofuna ndi malangizo abwino aza mmene tingagonjetsere tchimo.

MA SITEPE OGONJETSERA UCHIMO

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Chifukwa choti tonse tasiya kukhala mchere , kodi tingapangidwenso bwanji kukhalanso mchere?. Kodi tilibenso ntchito ndipo tiyenera kukaponyedwa ndikupondedwa? Ngakhale machimo athu angakhale akulu , baibulo likutiiza kuti malangizo a mmene tingachotsere machimo ndikutisimikizila kuti mphanvu ya Mulungu ikhodza kugonjetsa tchimo lathu lonse . Mphanvu yake ikhodza kutipangitsanso kukhala ndi mchere!.

MMaphunziro athu awiri omwe akubwerawa , tiphunzira za ndondomeko zitatatu zogonjetsera uchimo mmoyo mwathu:.

1. Kuchotsa uchimo.
2. Kukonzanso malingaliro athu , komanso.
3. Kuchotsa zoipa , kuika zabwino.

Kuchotsa Uchimo

Malangizo kwa Mphunzitsi: Pamene mukuphunzitsa maphunziro awiri otsatirawa , lembani nambala ina iliyonse ndi mutu wa nkhanu pa positala kapena pa bolodi yoyera . Ndipo onetsani **ZINTHUNZI** zomwe zikuonetsa mfundo yatsopanoyi. Ndipo pitirilani kufotokoza chilli chonse. Mutafotokoza china chilichonse , unikalani mfundo zakale zija kuti anthu azikumbukila ma sitepe onse. Palinso peji ina yophera mphongo mu **BUKHU LA OPHUNZIRA** pa ma sitepe onse 9 ndi malemba otsatirawa. Tiyezi tione masitepe atatu akuchotsa uchimo.

1. Zindikilani tchimolo : (**ZINTHUNZI**: Dzanja lomwe li ndi dontho lakuda.)

Mufunseni Mulungu kuti akuonetsereni mwapaderadera tchimo lomwe lilipo pa moyo wanu lomwe akufuna kuti inu muganizilepo kulikonza , kulichotsa. Likhodza kukhala zinthu zomwe timachita , monga mabodza , kapena chinachake chomwe tikulephera kuchita- monga kukonda anthu ena monga akazi athu monga mmene khristu anakonderanso mpingo.



Tikuona Davidi akuchita izi mu Masalimo 139:23-24 , imene ikunena kuti , “ Ndifufudzeni ine , Ambuye , ndikudziwa mtima wanga , ndiyetseni ine ndikudziwa malingaliro anga . ndioneni ngati pali njira yachitaiko mwa ine , ndipo munditsogolere mu njira yamuyaya’

2. Vomerezani machimo ndi kukhululukiridwa (**ZINTHUNZI**: Mau amakolana ndi madontho akudwa mkati.)


Tchimolo likangodzindikilika , timalivomereza tchimolo kwa Mulungu kwa Mulungu komanso kwa anthu ena, 1 Yohane 1:9 imati , “ Ngati tivomereza machimo athu , iye ndiokhulupirika , ndiwachilungamo ndipo azatikhululukila machimo athu ndikutilungamitsa ku machimo athu ndikutichotsera kusalungama kwathu konse. “ Khalani olimbika mtima- palibe tchimo lomwe liri lalikulu pamaso pa Mulungu! Iye ndiokhulupirika kuti atikhululukire machimo athu onse.



Ngati tamuchimwira wina wake , ndizabwino kuti munthuyo atikhululukire, ngati ubwenzi waonongeka kapena kupasuka ndi uchimo wathu , ndi zofunikira kwambiri kuti tivomereze ndikupempha chikhululukiko ndi cholinga choti ubwenzi wathu upitirile.

3. Lapani (**ZINTHUNZI**: Cholankhulira chokhala ndi dontho lakuda lokhala ndi mizere pakati pake.)

Kodi ndi chofunikira kulapa ndi cholinga choti musazachitenso uchimowo. Kulapa kumatanthauza kale kuti kuchoka njira ya uchimo ndikuyang'ana kwa Mulungu ndi chifuniro chake.



Mu Yobu 31:1 , tikuwerenga kuti “ Ndinapanga phangano ndimaso anga kuti ndisayang'anenso mwachilakolako mkazi . ‘ Apa tikuona Yobu analapa ndikuzipereka kuti sazamuyang'anenso mzimayi ndi chilakolako. Yobu anali munthu amene Mulungu anamutcha kuti ndi “ opanda banga ndi wachiongoko (Yobu 1:8) Ndipo Yobu anachipeza chothandiza kuzipereka pa uchimo umenewu! Tiyamika ambuye kuti ndi iyeyo amene amatipanga kukhala olungama ndi oongoka!

KUKONZANSO MALINGALIRO ATHU

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Ndiye tiyezi tione ma sitepe atatu amene angakuthandizeni kukonzanso malingaliro athu.

4. Pempherani Tsiku ndi Tsiku : ZITHUNZI: Manja akupephera.)

Sitingagonjetse tchimo patokha ndi mphanvu zathu. Ngakhale mtumwi Paulo ananenanso ku bukhu la aroma 7:19-20 , “ Chifukwa sindimachita zabwino zomwe ndikufuna kuchita , koma zoipa zomwe sindikufuna kuchita. “Ndiye ngati ndichita zomwe sindikufuna kuchita, ndiye kuti sindinenso amene ndikuchita zinthuzo , siine amene ndikuchita , koma ndi tchimo limene lili mwa ine lomwe limachita zinthuzo.



Timafunikila thandizo la Mulungu kuti tichotse uchimo ku mtima. Chifukwa choti tikudziwa kuti tsiku lina lililonse tizakumana ndi mayesero , tsiku lina lililonse tikuyenera tizikonzekeretse tokha popemphera kwa Mulungu kuti atithandize. Izi zikutikumbutsa za kudalira kwathu pa Mulungu komanso pa kudzipoleka kwathu kwa Iye. Tikuyenera kutsatira malangizo amene Yesu anapeleka kwa Ophunzira ake , “ Mateyu , yang’anitsitsani ndi kupemphera kuti musagwe mmayesero , “Mateyu 26:41).

Kupemphera mosalekeza kumatilumikiza ndi iye amene ali wamphanvu zokwanitsa kugonjetsa machimo athu . iye anagonjetsa kale uchimo ndi imfa , kuti tikadalire Mulungu ndikugonjetsa tchimo pa moyo wathu!

5. Kulumulira kaganizidwe kathu (ZITHUNZI: Baluni ya maganizo ozaza ndi ma dontho opanda kanthu).

Tchimo lina lililonse limachitika kawiri – kamodzi mmalingaliro mwathu ndipo kachiwiri mu khalidwe lthu. Ndiyeno , choyamba tikuyenera kulumulira maganizo athu ndicholinga choti tipewe uchimo umene uli mmaganizo athu kukhala chochitika cha uchimo.



Werengani ma vesi otsatirawa:

Aroma 12:” , “ Musatengere zochitika za ziko lino lapansi , koma musinthike pokonzanso malingaliro anu. Kenako muzakwanitsa kulawa ndikutsimikiza chifuniro cha Mulungu- Iye ndiwabwino , okondweretsa , ndiwachifuniro chabwino!.


2 Akorinto 10:5b..... Timaika pa ukapolo malingaliro ena aliwonse kuti azikhala onvera kwa Khristu.

Afilipo 4:8 , “ “ Komaliza , abale ndi alongo , chilichonse chomwe ndi choona , chilichonse chomwe ndichabwino , chilichonse chomwe ndicholondola , chilichonse chomwe ndi chokondeka , chilichonse chomwe ndichosililika – ngati chinachilichonse ndichanwiro ndi choyenera kuyamikidwa , ganizani zimenezo.

Kodi tingaike bwanji malingaliro athu onse pa ukapolo? Tikaganizila malingaliro ochimwa(mwa chisanzo , junga ,” ndimagwira ntchito molimbika koma banja langa silimayamikila mphanvu zomwe ndimaikapo pa miyoyo yawo , ‘ndimasankha kugwira tchito monga kwa Mulungu ndi ulemelero wake Sindikuyembekezeranso kuyamikidwa kuchokera ku banja langa , koma ndiyesetsa kumusangalatsa Mulungu. Pamene Mukupitirizabe ndi tsiku lanu . Bwerezani izi pamene malingalilo a uchimo aja akutulukabe- Mulungu samatopa potikhululukira ndipotipatsa zabwino.

6. Kuloweza malemba (ZITHUNZI: Baluni ya maganaizo amene ali ndi bukhu mkati mwake).

Kuloweza malemba kumatithandiza kuti tizitha kulamulira maganizo athu ndipo amathandizira choonadi kuti chikhadzikike mwa inu. Tikayamba kuganizira malingaliro olakwika, tikhodza kumakumbukira ma vesi amene tinawaloweza aja kuti akhale mmalingaliro mwathu. Mwa njira imeneyi , timakonzanso malingaliro athu pochotsa icho chimene ndichoipa ndikuika icho chimene ndichabwino.



Pamene Yesu analowa kuchipululu ndipo tsatana anabwera kuzamuyetsa. Yesu anatenga malemba mkumulankhulira ndi cholinga choti amugonjetsere mayesero ake. Masalimo 119:11 imayi , “ Ndabisa mawu anu mu mtima mwanga kuti ndisachimwenso

Baibulo limaulutsiratu kuti kuloweza malemba a mbaibulo kumathandiza kugonjetsa uchimo. Tikhodza kupeza gawo lina lake la malemba lomwe likufananila ndi uchimo lomwe tikuyesetsa kuligonjetsalo. Ngati simukudziwa kuti mukapeza kuti malemba. Funsani abusa kapena mzanu amene akhodza kukutsogolerani. Lowezani malemba , ndipo zizakuthandizani kugonjetsa mayesero amene angabwerenso.

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU

Malangizo kwa Mphunzitsi:*Hold up an image and have the class call out what step it represents. For example, hold up the image of the hand with the black dot on it and participants shout out, ‘Identify the sin!’ You can keep score if you’d like to make it more competitive: the first person to call out the step that the image represents wins a point!*

MATHERO

Tonsefe tinachimwa mmitima yathu. Palibe wina aliyense amene ali opanda banga , kapena oyera. Zifooko za machimo athu anachapika mu mchere: tchimo limachotsa mchere wathu . Mulungu amafuna kutikhululukila zochimwa zathu. Kuchotsa tchimo mmoyo wathu kumatithandiza kuchotsa uchimo mmoyo wathu ndikutipanga kukhalanso ndi mchere miyoyo yathu. Ndipo izi zimatilola kuti tikhale ochitachita ndi opindulitsanso pamaso pa Mulungu pochita ntchito zachikondi mu dera lathu.

Kugonjetsa tchimo mmoyo mwathu kumachita bwino ndipo zimayenda bwino. Taona lero kuti kugonjetsa tchimo kumachitika choyamba pa kuchotsa tchimo kenako kukonzanso malingaliro athu. Izi ndi zinthu zimene zimatenga nthawi kwambiri , koma khalani olimbika. Yesu watigonjetsera kale uchimo ndi imfa! Mphanvu yake ikhodza kugonjetsa uchimo miyoyo yathunso.

Phunziro 5: Kuchotsa zoipa kuika zabwino

Mfundo zenizeni:

- Kuchotsa zikhalidwe zoipa ndi kuika zikhalidwe zabwino ndi kofunika kugonjetsa uchimo mmoyo wathu wa tsiku ndi tsiku.
- Tikuyenera kutenga mbali kuthana ndi uchimo ndi cholinga choti tikhale mchere ndi kuunika mu dera lathu.

Zofunika :

- Buku la ophunzira: Tebulo la kugonjetsa uchimo- chitsanzo cha kudandaula ndi tebulo yopanda kanthu(pangani kope imodzi pa munthu wina aliynse/ gulu lililonse). Shiti imeneyi imapezekanso pamapeto pa bukhu la aphunzitsili.
- **Zithunzi** : Zithunzi za sitepe 6-9 , kugonjetsa uchimo (onse atatu).

Chiyambi

Mu phunziro lomwe langothali , tinasewera sewero lotikumbutsa zoti tonsefe tili ndi machimo mmitima mwathu. Tinaona kuti tikuyenera kugonjetsa uchimo pochotsa uchimowo ndikukonzanso malingaliro athu. Tsopano tikuona za kuchotsa zikhalidwe zoipa za njira yathu ya uchimo.

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU

Malangizo kwa Mphunzitsi: Nkhani iyi , mukhoza kungoiwerenga kapena kuchitidwa ngati sewero ndi anthu amene akutenga nawo mbali pamene mukuwerenga nkhanayi..

Tanverani ka nkhanika aka...

Panali munthu amene amamanga nyumba. Amati akapeza ndalama zokwanira , amayesesa kuimangako ma laini angapo pa nthawiyo. Mmene nyumba ija inatha , anakonzanso zosamusa banja lake ndikukakhala mu nyumba imeneyi . Ohh , amayembekezera koposa kufika pa tsiku limeneli lomwe akukakhala mu nyumba imeneyi, koma panalinso ka vuto kamodzi; chifukwa choti amakhala cha patalipo , sanali pafupi kuti akhoza kumayang'anira nyumba yake yatsopanoyi tsiku ndi tsiku , ichi chinapeleka vuto kwa mkosana ameneyi ndithu.

Poyamba , makoma asanathe , amatha kubwera kunyumbayi kuzamva kwa neba mbuzi zawo zimadya panja ndi nyumba momwe. Ili silinali vuto kwambiri , komabe panali chisokonezo.bamboyu anamaliza khomalo ndikuika chitseko kuti nyama sizimakwanitsa kulowa.

Patatha masabata angapo , anabweranso pa ntchitoyi ndikupeza kuti banja la makoswe laika zitsa zake pa ngodya pena pake . Anachotsa makoswewo ndikumalizitsa denga la nyumbayi , kuganiza kuti ichi chiletsa makoswe kuti asalowe.

Nthawi ina , anafikanso panyumbayo ndikuzapeza kuti pali anamzeze ambiri amene amanga zitsa zawo ndikumakhala mnyumbamo!Anachotsa ananzenzewo ndikuchotsa zitsa zomwe amakhala.

Kenanso , anabwera kunyumba kwake , kupeza kuti pali mzimayi wina oyandikana naye amene wayamba bizinesi yake yogulitsa kachaso kwa azibambo a mmudzimu. Pokwiya kuti nyumba yake ikugwiritsidwa ntchito opanda chilolezo , Analamula kuti mzimayiyu asamuke ndi bizinesi yakeyo. Ndipo anatseka zitseko zija ndi loko namapita.

Patatha miyezi ingapo , kachikena , mzibambo wina anabwera ndikuswa loko uja ndikumakhala mmenemo , anali mzibambo wachilendo , mwini wake pobwera anapeza loko wangolendewera pa ma hinjizi. Munthuyu

anali wamavuvu komanso oledzera. Anaononga zambiri mkati mwa nyumbayi ndipo analonjeza kumenya mwini wake nyumbayo. Mwini wakeyu anagwiritsa ntchito mafumu a mmudzi kuti amuchotse bambo wachilendoyi.

Pa mapeto , munthuyo anazindikila kuti , ngati nyumba yake ikhalebe yopanda kanthu , china chake chikhoza kulowamo ndikukakhadzika , zachiziwikile kuti chomwe chingalowemo ndi zirombo zosakhala bwino ndi anthu amene analibe zolinga zabwino konse. Anaganiza kuti asankhe anthu omwe angakhalemo , banja lodekha lomwe likhoza kumakhalamo ndikumayang'anira nyumbayo kufikira pamene eni wakewo atalowamo mnyumbamo.

Miyezi inapita ndipo munthu anabwera kuzafuna kuti amalizetse ndime zina zotsatirazo pa chikonzekeretso cha nyumbayo. Anali okondwa pobwera kupeza kuti banjalo linasamalira bwino nyumbayo! Chitseko chinali mmalo mwake , mazenera anakolekedwa bwinobwino ndi kamsalu kotchinga kuti fumbi lisalowe , anachotsa chiswe chonse chomwe chinali mnyumbamo , ndiponso panja pamasesedwanso bwinobwino.

- Kodi ndi chani chomwe chinachitika pamene nyumba inangosiyidwa yokha yokha?.
- Kodi ndi chani chimene mwini nyumba anachita kuti zirombo ndi anthu asalowe?.
- Kodi ndi chani chomwe taphunzira kudzera mu nkhani imeneyi?.

Munthu mu nkhanayi amachotsa zilombozo nthawi zonse ndikukonzanso nyumba yake ndikuonetsetsa kuti zisabwerenso , koma nthawi ina iliyonse amati akachita zimenezi ndikukabweranso , amapeza kuti zilombo zina zalowanso , kufikila pamene anayenera kupeza wina amene akuyenera kukhalamo ndithu ndikumasamalira.

Mitima yathu ndi malingaliro ali ngati a nyumba ya munthu ameneyu. Kawirikawiri timagonjetsa uchimo mbali imodzi kupeza kuti yesero linanso lalowa. Monga munthu amene ali mu nkhanayi , tikuyenera kumalizitsa ntchito ya kugonjetsa uchimo mmoyo mwathu pochotsa makhalidwe oipa ndikuikamo makhalidwe abwino. Kudzadza moyo wathu ndi zinthu zabwino zochokera kwa Mulungu ndi choonadi chake ndi chikondi chake ndiye chitetezo chabwino kwambiri cholimbanilana ndi uchimo omwe ukubwera ku moyo wathu mmitima mwathu.

Tatiyeni tione ma sitepe atatu omalizila ogonjetsera machimo.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Mwachangu taunikilani ma sitepe 6 amene tinawaphunzira kufikila pa nthawi ino. Phunzitsani mfundo zotsatirazi kuchokera pa positala ndikuwauza anthu za chithunzi ichi musanasunthile ku mfundo yotsatira.

Kuchotsa zoipa ndikuika zabwino

KUKAMBIKANA KWA MMAGULU AKULUAKULU


7. **Thawani ku mayesero (ZITHUNZI)** Munthu amene akuthawa dontho lakuda). Kugonjetsa tchimo kuli ngati nkondo . Mu nkondo ,mukuyenera kumudziwa mdani wanu. Kugonjetsa uchimo sikosiyana ayi. Tikuyenera kudzidziwa tokha ndi kufooka kwathu. Yakobo 4:7 amati, “ **Gonjerani tsopano , kwa Mulungu. Kanani zoipa , ndipo iye azakuchokerani.**”



Pewani Machimo . Ngati muli ndi vuto la kumwa mowa , musapitenso ku bala kokacheza ndi anzanu. Ngati muli ndi vuto la Nsanje ndiye kuti mukuyenera kusiya china chilichonse chomwe chimakupangitsani kuchita Nsanje kufikila pamene mutaima pamalo oti mukhoza kuthokoza ndi chinthu chomwe Mulungu wakupatsani. Limbikitsikani ndi 1 Akorinto 10:13 ; ‘ Palibe themberelo lomwe lingaposere msinkhu wanu . Ndipo Mulungu ndiokhulupirika , sadzakulolani kuti muyesedwe kopyolera msinkhu wanu. Koma mukayesedwa , Azapeleka njira yothawira koma mukwanitse kutulukanso.


8. **Yambani zikhalidwe zabwino (ZITHUNZI).** Munthu amene anali ndi banga lakuda kuikidwa banga lomwe ndi loyera.

Mwa chitsanzo , ngati ndilapa mchitidwe omangokwiya ndikafika kunyumba ndikupeza kuti mkazi wanga sanaphike chakudya , ndingathe kusintha khalidwe pomamufunsa kuti kodi ndi chani chomwe tingachite kuti zinthu zonse zikhale bwino. Ngati ndikusiya kukhala ndi anzanga ku bala usiku wina uliwonse , ndikhoza kuikapo chikhalidwe chomakhala ndikucheza ndi ana anga usiku wina uliwonse. Ngati ndili ndi mchitidwe omangodandaula kapena kukhumudwa , ndikuyenera kuyamba kukhala ndi chikhalidwe chomakumbukira ndi kuyamika Mulungu pa zinthu zingapo zazikulu zomwe Mulungu wandipatsa pa tsiku limenelo.



9. **Kuonetsera poyera: ZITHUNZI).** Anthu awiri amene agwirana mothandizana amene onse ali ndi banga loyera pamtima pawo. Ichitu ndi chofunika ngati tifuna kugonjetsa tchimo!.

Pamene tikupanga chisankho chabwino ndikuyamba kuchita zikhalidwe zabwino kuti mupewe tchimo , zizakhala zophweka kuti mugonjetse tchimo , nthawi zonse tikapanga zisankho zoyenera , zimakhala zinthu zophweka kwambiri. Kukhazikitsa chikhalidwe chochita zinthu zabwino kumakhala kophweka ngati tikhala ndi mzanthu wina amene amatithangatila kutilimbikitsa mmoyo wa tsiku ndi tsiku. Pezani wina wake amene azakhale okuwerengelani zomwe munanena kuti mukufuna zikwanilitsedwe ndi kuonetsetsa kuti mukuchita zinthu zoyenera kukafikira ku zinthu zomwe mukuyembekzera kuti zichitikezo.



Chifukwa choti kugonjetsa tchimo ndi kovuta , tikufunikila anzathu awiri kapena atatu amene angatithandize kugonjetsa tchimo. Anthu amenewa akuyeneranso kukhala anthu okhulupirira ndi wachiyero amene tikhoza kumagawana naye kuzipereka kwathu pa moyo wathu okhala mu chiyero. Iwonso , akuyenera akhale amene ali mbali imodzi yomwe akulimbana ndi uchimo miyoyo yawo ndipo akuyenera kukhala ndi mtima oti akhoza kukuuzaninso za momwe akulimbanila ndi kuthana ndi uchimo.

KUUNIKILA PA NOKHA.

Werengani Mlaliki 4:9–10.

‘Awiri aposa mmodzi , chifukwa ali ndi phindu labwino pa ntchito ya manja awo; ngati modzi akugwa , mzakeyo akhoza kumudzutsanso. Koma tsoka kwa iye amene agwa koma alibe munthu oti akhoza kumuthandiza kudzuka.

- Pempherani ndikumufunsa Mulungu kuti akuonetseni amene mukhoza kumapemphera naye pafupipafupi ndikumapatsana chilimbikitsa pamene nonse mukugwira ntchito yolimbana ndi uchimo ndi mayesero.

CHOCHITIKA CHA PA GULU (Ngati mungafune): Ngati gulu lanu ndi lophunzira kuti likhoza kutha kuwerenga komanso limakonda kumawerenga malemba bwinobwino , mukhoza kukonza magulu kuti ayang’ane ma vesi awa ndikuyankha funso loti “Kodi ndi njira zina ziti zomwe tingagwiritse ntchito kuthandizana polimbana ndi uchimo?.

- Akolose 3:16 – Kuphunzitsa ndi kuyamikila.
- Aheberi 3:13 –*Kulimbikitsa*.
- Yakobo 5:16 – Kuvomereza ndi kupemphera.
- Agalatiya 6:2 – Senzani mtolo wa wina ndi mzake.
- Aefeso 4:29 –Mangililanani wina ndi nzake molingana ndi zosowa zanonse.

Kuyesera Kugonjetsa Uchimo

CHOCHITIKA CHA MMAGULU ANG'ONOANG'ONO

Malangizo kwa Mphunzitsi: Onetserani ku gulu lonse kuti kodi ma sitepe 9 onsewa akhoza kugwiritsidwa ntchito motni pamene tikulimbana ndi kugonjetsa tchimo la mtundu wina wake(Kudandaula ndi chitsanzo cha chinthu chimenechi chomwe chaonetsedwa pa tebulo ya ma sampulo pa mapeto pa phunziro limeneli.

- Kodi ndi machimo ati 4 kapena 5 amene amapezeka mu dera lino?.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Gulu likatha kupeza ndi kuzindikila machimo 4 kapena 5 amene amachitika mu dera lawo , ndiye kenako gawanani mmagulu ndipo muike mu gulu lina lililonse kuti akambirane . Mu gulumo akambirane sitepe ina iliyonse pa tchimo limene iwo aikilidwa.

- Gwiritsani ntchito **BUKHU LA OPHUNZIRA** kuti muganizile za mmene mungagwiritsire ntchito ma sitepe 9 onse amene alipo akugonjetsa machimo amene atchulidwawa.

PELEKANI LIPOTI





MATHERO






KUUNIKILA PATOKHA

Pempherani ndi kumufunsa Mulungu kuti akuonetseni tchimo limene akufuna kuti inu muligonjezetse. Tenganipo nthawi kumunvetsera kuti iye apekeke chinachake mmalingaliro mwanu. Ndiye mufunseni kuti akuthandizeni kutsatira ma sitepe ogonjetsera tchimolo.

KUGONJETA UTCHIMO

TEBULO YA CHITSANZO- Kudandaula

MA SITEPE. S	CHITHUNZI	TCHIMO
Kuchotsa tchimo		
1. Kudzindikira		Kudandaula
2. Kuvomereza ndi kukhululuka		Ndikuvomereza kuti ndimadandaula za kugwira ntchito molimbika. Chonde ndikhululukileni chifukwa chakudandaula.
3. Lapani		Sindikufuna mtima umene uzidandaulanso . Mmalo mwake mwakudandaula , ndikufuna ndilankhule zabwino zokhazokha za kuthokoza pa zimene ndili nazo.
KUKONZANSO MALINGALIRO ATHU		
4. Pempherani tsiku ndi tsiku.		Ndikufuna thandizo lero kuti ndisadandaulenso. Ndithandizeni kuti ndithokozeni ndikugwira ntchito mokondwera.

5. Lamulirani kuganiza kwanu.		Ndikamadandaula , ndimangoganizira chabe za ine ndekha. Mmalo mwake , ndikuyenera ndidziganiza za mmene ntchito imene ili pa tsogolo pangayi ndingaikwanilitse motani kuti ikalemekeze Mulungu. Ndikufunikira kuti ndiganizire za iye osati za ine ndekha ayi.
6. Lowezani malemba.		Aefeso 4:29 imati:’ Musalore kuti kulankhula kosalungama kwina kulikonse kutuluke pakamwa panu , koma chokhacho chomwe chilli chothandiza kumangilira wina ndi nzake , kuti chikapindulire iwo amene akumvetsera.”
CHOTSANI ZOIPA KUIKA ZABWINO		
7. Thawani mayesero.		Nthawi zonse ndimadandaula ndikakhala ndi _____. Sindimafuna konse kuti ndikhale ndi nthawi yochuluka ndi iye ndikumuuza kuti sindifuna kudandaulanso za iye.
7. Khazikitsani zikhalidwe zabwino.		Ngati ndayesedwa kuti ndiyambe kudandaula , ndiziganizira zinthu zitatu zomwe ndikumuyamika nazo Mulungu. Ndizimuyamika Mulungu kuti akhoza kugwiritsa ntchito nyengo zanga kuti zimubweretsere Ulemelero.
9. Kuonetsa Poyera.		Ndimuza _____ za khumbo langa lakugonjetsa kudandaula. Ndimuza kuti azindiunikila ndi kuona mmene ndikuchitila pa chinthu chimenechi , ndipo akandifunsa , sindiyeseranso kubisa chinthu chimene ndachita. Ndifunanso kuthandiza kuona mmene iye akumenyera nkondo yolimbana ndi uchimo umenewu wake ngati angalole.

PHUNZIRO 6: KUKHALA MPINGO WA MCHERE NDI KUUNIKA

Mfundo zeni zeni:

1. Mpingo yathu yalamulidwa kuti ikhale mchere ndi kuunika ku Madera athu.
2. Ndi mphanvu ya Mulungu , mchere ndi kuunika zitha kusintha Madera athu.

ZIPANGIZO:

- Pepala ya positala kapena bolodi yoyela ndi pemto maka. .

Kodi titanganidwilanji kutumikila anthu ena?.

Mu ma phunziro atatu otsatirawa , tiyang'ana za mmene tingakhalire mpingo umene uli mchere ndi kuunika ku dera lathu.

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU ANG'ONOANG'ONO.

Mmagulu ang'ono ang'ono taganizilani zifukwa zochuluka zomwe a Khristu ndi mpingo akuyenera kukangalika ndi ntchito yotumikira anthu osauka. Taganizani zina za mbuyomo zomwe munaphunzira kuchokera ku phunziro loyamba kufikila lero . Ngati mkotheke , kumbukilani ma vesi ena apaderadera.

PELEKANIKO LIPOTI

ZOFUNIKA KWA MPHUNZITSI: Gululi likamaliza kugawana ma notsi , onjezerani mfundo zinazi zomwe palibepo.

- *Mulungu anatuma Yesu kudzafa kuti alumikizitse maubale atatu amene anaphwanyika pamene Adam anachimwa. Ubale wathu ndi Mulungu , ubale wathu ndi anzathu , ubale wathu ndi chilengedwe. Ifenso taitanidwa ku utumiki omwe uja wa chiyanjanitso- kubweretsa machilitso ku ma ubale onse atatu amene anaphwanyika aja.*
- *Anthu ndiofunikila kwambiri pamaso pa Mulungu-kufika poti anatuma mwana wake obadwa yekha kuti adzatifere. Ifenso tikuyenera kusamalira anthu ena .*
- *Mu Yesaya 58 , Mulungu sanati samayankha mapemphero a mpingo chifukwa analephera kusamalira osauka komanso ana/azimayi amasiye.*
- *Pamene Paulo anaphera mphongo pa nkhanu ya chipangano chakale , katatu kamene anaphunzitsa kuti tikonde Mulungu ndikukondanso anansi athu- chifukwa umu ndi mmene timaonetserela chikondi chathu kwa Mulungu.*
- *Mu Fanizo la Msamaliya wa chifundo , msamaliya wa chifundo anamuyang'anira munthu amene anamenyedwa ndipo ndi msamaliyayo amene anapeleka chilichonse chomwe munthuyu anafunikila , sanamulalikile konse olo pangono.*
- *Pa chiphunzitso cha nkhoa ndi mbuzi , Yesu anaphunzitsa kuti tikuyenera kupeleka chakudya kwa anthu anjala , chokumwa kwa iwo amene ali ndi luzu , kuyendera odwala kapena iwo iwo amene ali mu ndende , ndikuveka amaliseche , tikachitira ichi munthu wina , zikhala ngati tikumuchitira Khristu Yesu.*
- *Taitanidwa kuti tikamange ufumu wa Mulungu. Zikutanthauza kuti tikufuna anthu ambiri abwere kwa Khristu Yesu ndipo akhrstu achulukile kumumvera Mulungu mu dera lina lililonse la Moyo wawo. Mulungu walonjeza kuti , tikamumvera , lye adzatidalitsa. lye watipatsa ndondomeko zoti titsate zomwe zikhoza kutithandiza kukweza miyoyo yathu. Tikuyenera kukhala omvera kwa iye.*

Tatengani nthawi yolingalira.

- Kodi mukukhulupirila kuti ndi udindo wa mpingo kusamalira anthu osauka ndikuonetsa chikondi cha Mulungu ku dera lawo?.

Ndichofunika kukhulupirira kuti kusamalira osauka ndikusintha Madera anthu si chinthu chomwe tikuyenera kuchita kusankhaso ayi. Ndi mbali imodzi ya tanthauza lakukhala mkhristu ndi njira inanso imodzi imene timaonetsera chikondi cha Mulungu.

Mudzi osinthika

KUKAMBIKANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Monga mmene tinaonera , ndizofunika kwambiri kutsatira malamulo a Mulungu okhudzana ndi kukonda anzathu. Mvetserani nkhani ya mpingo uwu umene unagwiritsa ntchito maphunziro okhudzana ndi TCT amenenso mwakhala mukuphunzira. Tatenganipo nthawi kuganizira chomwe amapanga ndikuti chinabweretsa kusintha kwa zinthu kotani.

NKHANI YENIYENI- MUDZI WOSINTHIKA

Pali mudzi wina umene uli kumudzi kwambiri , uli cha ku phiri ndipo ndiophweka , anthu akumudziko amakonda kupanga mowa wa mpunga ndikulima komanso kusuta fodya. Ukhondo kumudziko unali ochepa ndipo unali vuto , amasamba kamodzi pa mwezi , ndipo amasamba mmanja patalipatali kwambiri , ndipo analibe zimbudzi , ndipo analibenso mayenje otaila zinyalala. Zovala zawo zinali zong'ambika , ndipo ana samavala bwino.

Mu nkhani yachuma , mudziwu umavutika kwambiri. Kunalibeko msewu weniweni pakati pawo ndi msewu weniweni-kunali chabe njira zoti azidutsa ndi miyendo basi. Chifukwa cha chimenechi , anthu amangogulitsa zomwe iwo amatha kukolola komanso zimene akanatha kunyamula pa mutu mu ulendo wautali kupita ku msikako. Chifukwa choti samagulitsa kwambiri , zimawavuta kuti azilimanso.

Anthu a ku mudzi anali akhristu , koma anali asanaphunzire zambiri zokhudzana ndi Mulungu. Koma analibe mtsogoleri wa Mpingo , ndipo azibusa samapita kuderali chifukwa kunali kopanda misewu. Kuti muwayendere muyenera kusiya njinga yanu ku msewu ndikuyenda kwa maola atatu , kuyembekezera kuti ukamabwerela njinga uipeza pomwepo ndipo sinabedwe! Analibe malo okumanilapo , ndipo samakula moyo wa uzimu konse.

Mpingo unanva za pulogalamu ya TCT ndikupempha Mtsogoleri wa mudera lawo kuti iwo akakhale nawo ku maphunzirowa. Kwa nthawi yaitali panalibe mmodzi mwa ophunzitsawo amene amkafuna kupita ku malo amenewa- unali ulendo wautali komanso ovuta kwambiri. Ngakhale anapita ku mudziko , ukhondo kunalibe ndipo amadziwa kuti akanatha kudwala. Komabe , Mulungu analankhula ndi modzi mwa ophunzitsawo ndipo iye anavomereza kuti apitako ndithu.

Mpingowu unayamba kuphunzira za TCT . Ntchito imodzi yomwe Mulungu anawaunikila kuti ayambe ndi kukulitsa msewu umene anthu amagwiritsa ntchito ku mudziko kupita ku msewu weniweni- ulendo wa ma kilomita 10 kudzera mmapiri. Anamvera Mulungu ndipo anakulitsa msewuwo pogwiritsa ntchito makasu ndi zipangizo zina zapamanja. Inali ntchito ya kalavula gaga , koma Mulungu anawadalitsa kwambiri. Zosatila zake msewu umenewu , mtengo wa zokolola zawo unakwera chifukwa amakwanitsa kumapita ndi zokololazo ku misika ya kutali posatila kuti panali msewu wabwino kwambiri.—Samayeneranso kunyamula zokolola zawo pamutu kapena paphewa . chifukwa amapeza phindu lochuluka , iwo anakopeka mtima kuti apitilize kugwira ntchito molimbikila kwambiri ndikumamwa mochepa. Anthu anayamba kulimbikila kugwira ntchito mmaminda mwawo , kumalima ndikumagulitsa mwina ka khumi kuposa mmene amakololera poyamba!.

Mudziwu si umodzinso mwa midzi imene ili yosatukuka , koma ukukula mwachanga kwambiri . chifukwa mpingo unagwiritsa ntchito chiphunzitsa cha zaumoyo cha TCT ndikuphunzitsanso zomwezi ku dera lawo , wina aliyense akudziwa mmene angathangatile munthu amene akudwala matenda ena ndi ena ang'ono ang'onowa , ndipo wina aliyense ali ndi chimbudzi , komanso munda wa masamba!. Mpingo unayamba kuchitisa maphunziro akwacha . Ndipo poona chidwi chomwe anthuwa anali nacho, Boma linawamangila sukulu . Mulungunso wawadalitsa ndi magetsi posalingalira kuti mamidzi ena ozungulila pano alibenso magetsi.

Mudziwu ndi wachisanzo kwa anthu ambiri amene awazungulira poona mmene Mulungu wasinthila ndi kubweretsa madalitso ochuluka pa miyoyo ya anthu. Atafunsidwa pokutha pa zaka zitatu kuti kodi achita ntchito zingati zachikondi pa zakazi , sanakwanitsenso kuwerengela zonsezi. Ngakhale atafunsidwa kuti apanga zingati miyezi itatu yomwe yangothayi , zinali zinthu zambiri kuti azitchule. MMalo mwake , amafotokoza kuti amkachita ntchito yachikondi imodzi kapena ziwiri pa sabata ina iliyonse ndipo pano ndi chikhaliwe chawo. Ngati akuona chomwe chikuyenera kuchitika , amangonyamuka ndikumachita chimenecho.

- Kodi ntchito za chikondi zinasintha bwanji mudziwu?.
- Kodi nanga mpingo umodzi , umene chidziwitso chawo ndi chochepa pa zinthu za Mulungu , akwanitsa bwanji kusintha mudzi wawo onse?.
 - *Anachita chomwe Mulungu anawaonetsa kuti achite.*
 - *Anali ndi machawi pochita chomwe amaphunzira.*
- Kodi mpingowu wakusunthani motani inuyo monga mpingo wanu?.

MOMWE MUNGABWERETSERE KUSINTHA

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Mipingo imene yaona kusintha kwabmiri mmadera awo ndi mipingo imene inazipeleka kuchita ntchito zachikondi – zazikulu komanso zazing'ono- ndikuzichita pafupipafupi , mwina pamwezi wina uliwonse , kapena pokutha pa masabata awiri!.

Tatiyeni tione njira 4 zomwe ife monga mpingo tikhoza kuthandizila kubweretsa kusintha ku Madera anthu.

Malangizo kwa Mphunzitsi: *Talembani ntchito zachikondi 4 pa bolodi ndikukonza positala ndikuitanila anthu ena kuti awerengenso.*

1. **Ntchito zachikondi zopangidwa ndi munthu paekha-** munthu mmodzi kutumikila banja lake kapena ma neba.
2. **Kapena ntchito zopangidwa ndi kagulu kakangono kapena mpingo-** Ma membala a mpingo amatenga mbali mu pulojekiti imene ikutenga masiku awiri kapena atatu kuti ithe.
3. **Ntchito za chikondi zazikulu** – Ntchito zazikuluko zomwe zimatenga masiku awiri, atatu zisanamalizike ndipo zimafunika anthu onse a mmderamo amene enawo ali kunja kwa mpingo. (Mwa chitsanzo , kukonza msewu).
4. **Maphunziro opitilira-** Kuphunzitsa ena za TCT .

CHOCHITIKA MMAGULU ANGONOANGONO

- Kodi mpingo wanu wachita kale chiyani kutumikila dera lanu lonse mu njira zonsezi?.
- Kodi mwaona kusintha kwanji mu dera lanu?.
- Kodi mwamuona Mulungu akukukwezani kapena kuchulukitsa ntchito za manja anu?.

KUPELEKA LIPOTI

Mukatha , itanani magulu ochepa kuti azapeleke maumboni awo pamaso pa gulu lonse.

MATHERO

Pamene tikumalizitsa lero , tikufuna titenge nthawi yathu kumuyamika Mulungu potithandiza kukwaniritsa chimene chachitika ndi kukuza komwe takuona kudzera mu zochitika zathu, tengani nthawi kumuyamika Mulungu , sankhani nyimbo za matamando kapena china chilichonse chomwe chingakuthandizeni kukhala okondwera mu mpingo wonse.

PHUNZIRO 7: MA SITEPE OTSATILA

Mfundo zazikulu:

1. Tikusowekera ntchito zachikondi zochuluka ngati tikuyenera kuona Madera athu akusintha.
2. Pemphero ndi gawo lofunikila kwambiri mu ntchito yakuchita ntchito zachikondi.

Zipangizo:

- Bukhu la ophunzira: ma sitepe akukonzera ntchito za chikondi.
- Positala ya ntchito zachikondi (konzani positala, kapena lembani pa bolodi).
- Positala yongopitilira kuphunzitsa (konzani positala kapena lembani pa bolodi).

KUUNIKILANSO

KUKAMBIKIRA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Kodi ndi ndani amene angakumbukile njira zinayi zakubweretsera kusintha zomwe tinaona mu phunziro lomwe langotha lija?.

1. **Ntchito zachikondi zopangidwa ndi munthu paekha-** munthu mmodzi kutumikila banja lake kapena ma neba.
2. **Kapena ntchito zopangidwa ndi kagulu kakangono kapena mpingo-** Ma membala a mpingo amatenga mbali mu pulojekiti imene ikutenga masiku awiri kapena atatu kuti ithe.
3. **Ntchito za chikondi zazikulu** – Ntchito zazikuluko zomwe zimatenga masiku awiri atatu zisanamalizike ndipo zimafunika anthu onse a mmdera amene enawo ali kunja kwa mpingo. (Mwa chitsanzo, kukonza msewu).
4. **Maphunziro opitilira-** Kuphunzitsa ena za TCT.

Lero tiona zinthu zina zomwe tingathe kuchita kuti zinthu izi tizione zikuchitika mu mpingo wathu.

Madera Anai

Werengani Luka 2:52.

- Kodi pali wina amene angakumbukile ma dera anayi amene Yesu anakulilamo?
 - Mzeru, msinkhu, muzimu (kukonderedwa ndi Mulungu), kukonderedwa ndi anthu!.
- Kodi ndi zitsanzo zina ziti za zosowa zomwe zili mmagawo amenewawa?
 - *Mzeru- mphunziro, kuphunzira maluso monga kuchilitsa matenda ena komanso kusamala ndalama.*
 - *Kuthupi- kusamalira thupi, manyumba okhadzikika, kukhala ndi chakudya, kukhala ndi madzi aukhondo!.*
 - *Uzimu- chipulumutso, kukhala chifupi ndi Mulungu.*
 - *Khalidwe – mabanja ndi kusunga maubale ndi maubwenzi, komanso maubale aku dera lathu!.*

Malangizo kwa Mphunzitsi: Lembani Madera anayiwa pa bolodi kapena bwerezani nonse pakamodzi kangapo kufikila pamene gulu lonse litaloweza mndandandawu.

Awa ndi Madera anayi amene Yesu anakuliramo, izinsu ndi zitsanzo zomwe mabanja athu, Madera athu akuyenera kukulira. Nthawi zina ndizotheka kukodwa mkumangochita ntchito yachikondi imodzimodzi- mwa chitsanzo, kumangopeleka zofuna zakuthupi za anthu kokha, kapena kumangowapempherela kokha anthu. Koma ngati tikufuna tione dera lathu likusintha, tikuyenera kuthandiza dera lathu ma gawo onse anayiwa.

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU ANG'ONOANG'ONO

Malangizo kwa Mphunzitsi: Agaweni anthu mmagulu ochepa , pa gulu lina lililonse muwapatseko dera limodzi kuchokera pa Luka 2:52- Gulu lina litenge mzeru ndi zathupi pamene gulu linalo litenge zauzimu komanso chikhalidwe. Takambiranani mafunso otsatirawa ku ma dera onse amene iwo apatsidwawo . pamene mukupeleka lipoti , dutsani mu dera lina lililonse pa nthawi ina iliyonse.

- Kodi ndi zinthu zina ziti zomwe mpingo wachita kale kutumikila dera lawo?.
- Kodi ndi zosowa zina ziti zomwe tikudzidziwa za mu dera lino?.
- Kodi ndi ziganizo zina ziti za ntchito za chikondi zomwe tikhoza kupanga kuti tithane ndi mabvuto amenewa?.

KUPELEKA LIPOTI

CHIPHUNZITSO CHONGOPITIRILA

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Mtundu wachinayi wa ntchito zathu zachikond ndiko “ kuphunzitsa kosalekeza”. Kuphunzitsa osalekeza ndi njira yabwino kwambiri ngati tikufuna tikhale mchere ndi kuunika . chimatambasula chidziwitso chatu kwa anthu amene ali naye pafupi cholinga choti anthu ambiri akakhale monga mmene Mulungu afunila kuti azikhalira.

Pali njira zambiri za momwe tingaphunzitsire mopitiramu.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Kwa magulu amene angathe kuwerenga , talembani pa bolodi kapena konzani positala ndikuitana ena kuti awerengenso bwinobwino. .

1. **Ziphunzitso ndi mauthenga ochokera kwa abusa** – azibusa ndi amene amalemekezedwa kuti ndi aphunzitsi mu mpingo komanso mu dera . kuonjezera apo amabweresanso chiphunzitso cha uzimu ndikumaulimbikisa mpingo , pali mwayi wambiri oti mukhoza kuphunzitsa pa za luso monga kulimbikitsa mabanja kapena kusamalira ana. Izi zikhoza kuchitika kudzera mu ma uthenga kapena mu ndondomeko yapadera ukatha uthenga kapena mwambo wa mapempherowo.
2. **Kuphunzitsana mtimagulu tating'ono-** kuphunzitsana mtimagulu kumathandiza kukuza moyo wa uzimu , kumaunikilana wina ndi mzake pamene tikupanga ntchito za chikondi ndikutumikila anzathu amene tayandikana nawo monga timagulu. Mmagulu angonowanso ndi malo oyenera kupanga kauniuni wa ma phunziro amene anaphunzitsidwa amene anthu ena sanamvetsetse kapena sanamve kumene. Wina aliyense wa ku magulu achinyamata ndi azimayi akhoza kupindula kudzera mmaphunzirowa akawamva.
3. **Maphunziro odziwika bwino a dera lonse-** mukhoza kutenga phunziroli kuchokera kwa azaumoyo , mabanja , kasamalidwe ka ndalama cholinga choti aphunzitsedwe kudzera ku ma sevisi achinyamata kapena mkati mwa sabata . Izi zimalola kuti akhristu ndi iwo amene Sali akhristu kuti aphunzire limodzi , kumanga ubale komanso kusegula makomo kuti anthu alumikizane.
4. **Mwayi wina ophunzitsa omwe sunali pa dongosolo** – pamene tikuyenda mu ulendo wa moyo , kuyendera odwala , kugwira ntchito kumunda , kusamalira ana , tikamamwa tiyi ndi mzathu – tikhoza kugawana chomwe tikuphunzira ndi anthu amene atizungulira . chitsanzo chimodzi ndi membala wa mpingo amene amagawa chiphunzitso pa ola limodzi kamodzi pa sabata kamodzi ndi anthu amene amagwila nawo ntchito mu filudi. Njira yabwino yolimbikitsira kuphunzitsana mmalo osiyanasiyana ndiko kulola kuti tiziphunzitsanso maphunziro amene anaphunzitsidwa ku kachisi cholinga choti anthu azikumbukila bwinobwino ndikuthandizanso ena amene mungakumane nawo mkati mwa sabatamu.

KAUNIUNI WA PAYEKHA NDI KUPEMPHERA

Tenganipo nthawi kupemphera ndi kumuza Mulungu mafunso awa. Kumbukilani kumvetsera kwa iye kuti akuonetseni choonadi ndikukupatsani ziganizo zatsopano.

- Kodi timaphunzitsa ena kangati pa zachimene taphunzira?.
- Kodi tingachulukitse bwanji mwayi oti tiphunzitse?kodi pali mwayi oti tikhoza kuphunzitsa chomwe sitinachione?.
- Kodi ndi zipangizo zanzi zomwe Mulungu watipatsa kuti tikhoza kuphunzitsira? Ndi chani chimene tikusowa?.

PELEKANI LIPOTI

Malangizo kwa Mphunzitsi: Gawanani mfundo . itanani onse otenga nawo mbali kuti alimbikitsane wina ndi mzake pogawana mmene aonera maphunziro amene akhala akuchitika. Aitaneni kuti nawonso apeleke maganizo awo okhudzana ndi Madera amene samachita bwino. Pelekani chilimbikitso pa kakulidwe mmadera amenewa.

KUKONZA NDONDOMEKO

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU

MALANGIZO PA CHOCHITIKA.

1. Ndiwerenga ma sitepe okhudzana ndi kupanga ndondomeko ya chochitika cha chikondi.
2. Wina aliyense amene ali ndi kuthekera , taimililani.
3. Nthawi zonse mukamva liwu lonena kuti , ‘pemphehani’ , gwadani kapena kupinda manja anu , kenako kuimililanso.
4. Tiyeni tiyesere limodzi.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Werengani mau amene awalitsidwawa, kutsindika , pa pemphero , nthawi zonse mukawerenga(mwa chitsanzo , ‘ Namba 1 , kukumana pafupipafupi .. Namba 2 , kupemphera limodzi , namba 3 unikalani zosowa ndi kupemphera , kalasi igwada kamodzi ndi kamodzi. Bwerezaninso chinthu ichi kachikena (kapenanso kachitatu). Kudutsa mu mfundo ina iliyonse , nthawi ina iliyonse , kuyenda mwa changu , Pokutha pa ichi , gululi lidzakhala likuzungulira uku ndi uku kupemphera.

- Kodi ndi chani chomwe chilili chofunika kwambiri pa kupanga ma pulani?.
- Pemphero!.

Mukhoza kukhala pansi tsopano pamene tikuwerenga mfundo izi. (Uzani wina aliyense kuti azinena nawo mfundozi. Ndiye funsani ozipeleka kuti awerenge mfundo ina iliyonse ya ntchito zachikondi , kupanga ma pulani Mu **Bukhu la ophunzira**. Kuwerenga ndi kufotokoza , kapena , ngati simukugwiritsa ntchito bukhu la ophunzira , ndiye werenganinso ndikufunsa mafunso kuti anthu abwerezenso mfundo zawozo.

1. **Kumanani pafupi pafupi** – Monga mpingo , mukuyenera kumakumana pafupi pafupi kuti mulunjike pa nchito za chikondi cholinga choti anthu asangotangwanidwa ndikuwaiwala. Yetsetsani kumakumana kosachepela kamodzi pa mwezi kupemphera , kukambirana ntchito zachikondi ndi kupanga ma pulani.
2. **Pemphehani limodzi** – Ndi kudzera mphanvu ya Mulungu ndi mzeru momwe tingasinthe Madera athu . ndi ntchito yosatheka pamene palibepo Mulungu , koma ngati tili ndi iye , tikhoza ndithu kubweretsa kusintha kwa mtundu wina. Musaiwale kufunika kwa pemphero , musanamizike kuganiza ngati zochitika zathu ndi zokwanila opanda pemphero!.
3. **Onani zosowa ndi kupemphera** - Munthu wina aliyense akuyenera kubwera atakonzeka kuzakambirana zosowa zomwe akuona mozungulira. Pamene mukuyenda mu tsiku lanu tsiku ndi tsiku , mukuyenera kumayang’ana zinthu zimene zikuyenera kumachitika kapena anthu amene akufunika thandizo . Mu kukumana kwanuku , kambiranani kuti chomwe chikufunika kuti chichitike ndi chani.

Pempherani limodzi kuti Mulungu akuonetseni chomwe mukuyenera kuchita ndikupanga ma Pulani omwe adzamubweretsera ulemelero.

4. **Pangani ma Pulani ndi kupemphera-** Mu zonse , ma pulani akuyenera kugwiritsa ntchito zipangizo zomwe Mulungu watipatsa kale ndipo tikwanitse kuziyendetsa kufikila pa chimalizilo cha mu nthawi yochepa. Komabe , chinthu chofunikila kwambiri ndichoti mu ma pulani anu musatilenso chimene Mulungu akukuonetsani kuti muchite . Baibulo limati ‘ njira za Mulungu si njira zathu , choncho akhoza kuti zina chinthu chimene sichikugwirizana ndi njira zathu koma chidzabweretsa zotsatira zamphanvu pamene zakwanilitsidwa. Ichi sichimapeleka tanthauzo konse kwa anthu amu nkhanayi kuti ayambe kumanga msewu – tinakakonda kwambiri kulangiza anthu kuti ayambe ndi ma pulojekiti ochepe. Komabe , kumeneku ndi kumene Mulungu watikankhila kuti tiyambile , monga mmene anachitila , zinadzetsa kusintha mu zotsatira zake kwakukulu ku mudziku.
5. **Pempherani ndi kuyambapo kuchita-** konzani tsiku ndi nthawi , ndikulemba zipangizo zomwe zikufunika kuti zigwire ntchito. Ndipo unikilani mu pulani yanu.
6. **Unikilani ndikupemphera momuthokozanso Mulungu-** Taonani kuti pakhala kukhudza kochuluka bwanji , ndipo mupeleke matamando kwa Mulungu chifukwa anali nanu kukuthandizani kumalizitsa ntchitoyo. Mu phunziro la kuonetsera chomwe mwachita , tidzaphunzira zambiri za mmene tingapangile sitepe imeneyi ndipo kuti tiunikile chiyani.

Kumbukilani : zochitika zazingono zomwe zachitika kawirikawiri zimakhala zabwino kwambiri kusiyanana ndi chinthu chochitika chachikulu chimene chimachitika kamodzi patatha nthawi yaitali!. Chochitika chachikulu chimodzi chimakhala bwino kwambiri koma ngati anthu sakuona mpingo ukuchita chinachake kwa nthawi yaitali , ndiye kuti chinthu chachikulucho chidzayamba kusiya kukhudza.

MATHERO

Mu phunziro lathu lotsatira , tidzapanganso ma pulani ena a ntchito zina za chikondi. Ngati mukuphunzira maphunziro amenewa pa sabata ina iliyonse , ndiye onetsetsani kuti mutengepo nthawi sabata ino kumufunsa Mulungu kuti ationetse zosowa zina mdera lathu zomwe monga gulu tikhodza kuzichia. Bwerani okonzekera kudzagawana naye chimene mwaona ndi chimene Mulungu wakhala akukuonetsani.

Ngati mukudumphura ku phunziro lina lija , ndiye taunikilani pa ma notsi anu okhudzana ndi phunziro limeneli . kodi ndi ziganizo zina ziti zomwe munazona mu chiphuzitso chimenechi?. Mufunсени Mulungu kuti akuonetseni kuti kodi ndi ziganizo zina ziti musanafike mu phunziro lina lotsatira.

PHUNZIRO 8 : NDONDOMEKO YA ZOCHITIKA ZATHU

Mfundo zeni zeni : Mwa pemphero ndi kuthandizidwa ndi Mulungu , tipanga pulani ya ntchito zathu zachikondi.

ZIPANGIZO:

- BUKHU LA OPHUNZIRA: MA SITEPE AKUKONZA NTCHITO ZA CHIKONDI.

KUKONZA PULANI

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Ndi ndani amene akukumbukira kapangidwe ka ma sitepe akukonzekera chochitika cha chikondi chomwe tinaona mu phunziro limeneli?.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Limbikitsani gulu kuti liyese ndi kukumbukila monga mmene angathere . akamaliza , werenganinso **Bukhu la ophunzira** , kachikena.

1. **Kumanani pafupi pafupi** – Monga mpingo , mukuyenera kumakumana pafupi pafupi kuti mulunjike pa ntchito za chikondi cholinga choti anthu asangotangwanidwa ndikuiwalaiwala. Yetsetsani mumakumana kosachepela kamodzi pa mwezi kupemphera , kukambirana ntchito zachikondi ndi kupanga ma pulani.
2. **Pempherani limodzi** – Ndi kudzera mphanvu ya Mulungu ndi mzeru momwe tingasinthe Madera athu . ndi ntchito yosatheka pamene palibepo Mulungu , koma ngati tili ndi iye , tikhoza ndithu kubweretsa kusintha kwa mtundu wina. Musaiwale kufunika kwa pemphero , musanamizike kuganiza ngati zochitika zathu ndi zokwanila opanda pemphero!.
3. **Onani zosowa ndi kupemphera** - Munthu wina aliyense akuyenera kubwera atakonzeka kuzakambirana zosowa zomwe akuona mozungulira. Pamene mukuyenda mu tsiku lanu tsiku ndi tsiku , mukuyenera kumayang’ana zinthu zimene zikuyenera kumachitika kapena anthu amene akufunika thandizo . Mu kukumana kwanuku , kambiranani kuti chomwe chikufunika kuti chichitike ndi chani. Pempherani limodzi kuti Mulungu akuonetseni chomwe mukuyenera kuchita ndikupanga ma Pulani omwe adzamubweretsa ulemelero.
4. **Pangani ma Pulani ndi kupemphera**- Mu zonse , ma pulani akuyenera kugwiritsa ntchito zipangizo zomwe Mulungu watipatsa kale ndipo tikwanitse kuziyendetsa kufikila pa chimalizilo cha mu nthawi yochepa. Komabe , chinthu chofunikira kwambiri ndichoti mu ma pulani anu musatilenso chimene Mulungu akukonetsani kuti muchite . Baibulo limati ‘ njira za Mulungu si njira zathu , choncho akhoza kuti zina chimene sichikugwirizana ndi njira zathu koma chizabweretsa zotsatira zamphanvu pamene zakwanilitsidwa. Ichi sichimapeleka tanthauzo konse kwa anthu amu nkhanayi kuti ayambe kumanga msewu – tinakakonda kwambiri kulangiza anthu kuti ayambe ndi ma pulojekiti ochepa. Komabe , kumeneku ndi kumene Mulungu watikankhila kuti tiyambile , monga mmene anachitila , zinadzetsa kusintha mu zotsatira zake kwakukulu ku mudziku.
5. **Pempherani ndi kuyambapo kuchita**- konzani tsiku ndi nthawi , ndikulemba zipangizo zomwe zikufunika kuti zigwire ntchito. Ndipo unikilininso mu pulani yanu.

6. **Unikilani ndikupemphera momuthokozanso Mulungu-** Taonani kuti pakhala kukhudza kochuluka bwanji , ndipo mupeleke matamando kwa Mulungu chifukwa anali nanu kukuthandizani kumalizitsa ntchitoyo. Mu phunziro la kuonetsera chomwe mwachita , tidzaphunzira zambiri za mmene tingapangile sitepe imeneyi ndipo kuti tiunikile chiyani.

Mu phunziro limenei , Tikufuna tiganizile chomwe Mulungu akhoza kutifunsa kuti tichite chotsatira . Ngati mukukumbukira nkhanu ya mudzi umene unasinthika , mukumbukiranso kuti kusintha konse kunayamba ndi anthu amene anamufunsa Mulungu kuti tichite chiyanu , ngakhale ntchitoyo inali yaikulu – kumanga mseu- iwo anakwanitsa. Zotsatirazo zinali zomwe sanaziyembekezere ; anaonjezera chuma chawo kuchuluka ka teni , ndipo anasiya kuledzera ndipo chidwi chawo chonse chinali pakuyenda mu kumvera kwa Mulungu mu dera lina lililonse la miyoyo yawo.

Ndiye , tiyeni tiyambe lero ndikupemphera ndikumufunsa Mulungu kuti atikumbutse zinthu zina zomwe angatiuze ife kuti tichite. Funsilani mzeru zake momwe mukuyang’ana pa mndandanda wa ziganizo zomwe mwaziika pa malo amodzi mmadera anayi a mu phunziro lomaliza ndi chimene Mulungu anakuonetsani pamene mumayendayenda mu sabata imeneyi.

PEMPHERO

Malangizo kwa Mphunzitsi: *Tsogolerani gulu mu nthawi ya kupemphera . Mutatha kumufunsa Mulungu kuti apeleke mzeru ndikukuonetseani zosowa zomwe akufuna kuti inu mukwanilitse. Tenganipo nthawi yachete. Pakatha mphindi zisanu , Mufunse Mulungu kuti mwakufuna kwake akutsogoleleni.*

Funsani gulu lonse kuti linene maganizo amene anabwera mmalingaliro mwawo pa nthawi imene anali chete . Ngati sichoncho , bwerelelani ndi kuunikila mndandanda umene munaupanga mu phunziro lomwe lapita lija ndikukaona ngati china mwa izo zikhoza kukhala malo abwino oyambirapo . Thandizani gulu kuti lipange chisankho pa nthawi yomwe ikuyenera kuyambika.

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Tsopano kuti mwaganizila pa ntchito yomwe mukuyenera kuichita tsopano titenga nthawi yathu kuti tipange pulani . Ganizilani mafunso awa pamene tikupanga ma Pulaniwa?.

1. Kodi pulojekiti iyamba liti?
2. Kodi pali zinthu zomwe zikufunikila ?. Kodi muzipeza bwanji?.
3. Kodi mufunika kuitanitsa anthu ena kuti atenge nawo mbali? Kodi ndi ndani amene achite chinthuchi?.
4. Kodi mukusowerekerera chilolezo kuchokera kwa wina wake?.

Kukhalabe Okhulupirika.

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Werengani Mateyu. 21:28-31.

- Kodi ndi chani chomwe chinachitika mu ndime imeneyi?.
- Kodi ndi mwana uti amene anachita chomwe atate amafuna?.
- *Mwana wachiwiri uja . Mwana oyamba anangowakondweretsa atate wake ndi mau koma analibe chiganizo choti amvere chomwe atate wawo anamuuuza kuti achite. Mwana wachiwiri uja anachita chomwe atate amafuna kuti chichitike kwa iye.*
 - *Kumbukilani kuti sizokwanila chabe kungokonzana ma Pulani , tikuyenera kuzilondola bwino bwino zonsezo..*

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

- Kodi pali chotchinga chomwe chingakulepheletseni kumalizitsa pulani yanuyi?.
- Kodi ndi chani chomwe mungapange kuti mugonjetse zophinja zimenezi?.

PEMPHERO

Tenganipo nthawi ndi kupemphera , kupeleka ma pulani anu onse kwa Mulungu ndikumufunsa kuti mukufuna thandizo lake pachikwanilitso cha ma pulaniwa.

MATHERO

KUKAMBILANA KWA MMAGULU ANG'ONO ANG'ONO

Mmagulu ang'ono ang'ono , taonani ngati mungathe kukumbukila mfundo ndi ganizo limodzi lalikulu mu phunziro lina lililonselo.

- Kodi ndi zinthu zina ziti zomwe mukufuna muchite mosiyana monga zotsatira za kuphunzira phunziro limeneli?.

KUPELEKA LIPOTI

Tiyeni titenge nthawi kumuyamika Mulungu pa zonse zomwe takonza ma pulani mu phunziro limeneli.

- Ndi ndani amene akufuna kupemphera ndikumufunsa Mulungu kuti akuthandizeni kuti zimene mwaziphunzirazo zizichitikadi?.

PHUNZIRO 9 : KUSAKA ANTHU OZIPELEKA

MFUNDO YENIYENI: Tikuyenera tilimbikitsane wina ndi mzake kuchita ntchito zabwino kudzera mu kuphunzitsa , kupanga mwayi , kuitana anthu kuti atenge nawo mbali , kuzindikila ena , kugwira ntchito limodzi, kumva kufunikila , ndi kusangalala.

ZIPANGIZOS:

- BUKHU LA OPHUNZIRA : Njira zisanu ndi ziwiri zakutumikila.
- BUKHU LA OPHUNZIRA : Mpingo omwe umatumikila.
- Tchatu , bolodi komanso ma pento maka.

Malangizo kwa Mphunzitsi: phunziro ili lakonzedwa chifukwa cha atsogoleri a mpingo amu mpingo mwanu , kuti liwathandize kuganizira za mmene angatengele anthu ambiri kubwera mu mpingo mwanu komanso kutumikika mu mpingo ndi mu dera za kuchita ntchito za chikondi.

CHIYAMBI : CHIKHALIDWE CHA KUTUMIKILA.

KUKAMBIKANA KWA MMAGULU AKULUAKULU

Mu 1 Akorinto 12 , Paulo akunena za thupi lonse . Akutikumbutsa kuti tonsefe ndife ziwalo za thupi limodzi ndipo , kuti thupi ligwire ntchito bwino , ziwalo zonse za thupilo zikuyenera kutenga nawo mbali pa kugwira ntchitoko . Komabe zikuonetsa kuti mpingo ina , ka gulu kena kake ka mu mpingo ndi kamene kakutanganidwa mu kutumikila pamene ena akungodikila kuti atumikilidwe. Muphunziro limeneli , tiyangani njira zambiri zosiyana za momwe tingapangitsire anthu kuti atenge nawo mbali mu kutumikila kapena iwo amene akutumikilawo kumva kulimbikitsika kuti akutumikila.

KUKAMBIKANA KWA MMAGULU ANG'ONO ANG'ONO

Tawerangani a Hebereri 10:24: 'Tatiyeni tsopano kuti tilimbikitsane motani pa zachikondi ndi ntchito zabwino. '

- Kodi ndi njira zanzi zina zomwe mungathe kugwiritsa ntchito kulimbikitsa anthu kuti azitenga nawo mbali mu kutumikila?. Kodi ndi chiti chimene chikuyenda bwino? Ndi chiti chomwe sichikuyenda bwino?.
- Kodi ndi ziganizo zina ziti zomwe muli nazo zopangira anthu ena kuti atenge nawo mbali ?.
- Kodi ndi chiyani chomwe mungapange kupangitsa anthu kuti azimva kukoma?.

PELEKANI LIPOTI

Mu phunziro lonseli , tiona maganizo seven pa za mmene tingalimbikitsire anthu ena kuti azitenga nawo mbali pa ntchito za chikondi.

NJIRA SEVENI ZAKULIMBIKITSIRA KUTUMIKILA

Malangizo kwa Mphunzitsi: Pamene mukulemba china chilichonsecho , lembani pa bolodi.

1. Phunzitsani za kufunika kwa kutumikila

Tikuyenera kuphunzitsa mmipingo mwathu za kufunika kuti tizitumikila . ngati anthu athu sakudziwa za maitanidwe a mulungu kuti anthu onse atumikile ma dera wo , ndiye tisadabwitsidwe ngati iwo sakutumikila.

2. KONZANI MWAYI

Pokonza zinthu monga ntchito za chikondi , timakhala tikukonza mwayi oti anthu a mu mpingo atenge nawo mbali pa kutumikila . chifukwa anthu ena kwa iwo ndi chovuta kuona chomwe iwo angachite.

Makamaka ngati sichinakhalebe chikhalidwe pa mpingopo. Yetsetsani kupanga mwayi oti anthu onse amene alili ndi ma luso osiyanasiyana mu mpingo apeze pamene akhoza kutenga nawo mbali. Funsani iwo kuti atulutse ziganizo zawo za chimene mpingo ukhoza kumachita .Mukhoza kudabwitsika ndi ma luso amene iwo ali nawo.

3. Itanani anthu kuti atenge nawo mbali

Anthu ambiri samazipeleka kuti atenge nawo mbali kufikila pamene mutawaitanitsa kuti atero. Akhoza kumvera pa gome za chimene chikuchitika , koma amayerekeza kuti anthu ena mu kachisimo ndiye amene angachite chinthuchi. Taonanionani mu mpingo anthu ena amene sapezeka ku ntchito za kutumikila komanso , pamene muli ndi chochitika cha chikondi kapena ntchito ya mtundu wina uliwonsewo, mukhoza kuona ntchito imene ikuyenerana ndi maluso awowo. Atengeleni nthawi yowaitana.

4. Zindikilani ndi kuwayamika anthu

Tonsefe timakonda kuthokozedwa ndi kuzindikilidwa ndi kuyamikidwa. Taonani mwa changu Aroma 16- pali maina ochuluka ndi zambiri zimene anthuwo anapanga. Tangoyerekezani anthu amene anatchulidwa mu kalata ameneyu anamva bwanji pozindikila kuti Paulo mtumwi anatchula maina awo mu bukhu lolemekezeka ngati ili?. Pamene maina amenewa akutikumbutsa za ntchito yolimbika imene anagwira , monga atsogoleri a mpingo , imatikumbutsanso za kufunika kozindikila ndi kuthokoza anthu ena . monga atsogoleri , tikuyenera kuti titengepo nthawi kuthokoza iwo amene akutumikila , makamaka kwa iwo amene samazindikilidwa kawirikawiri.

5. TSINDIKANI ZA KUFUNIKA

Werengani mateyu 25:34-40. Mu njira zambiri mu ndime imeneyi yapaderaderayi . Imatiuza kunena kuti china chilichonse chomwe timachita chochepa , Zili ngati tikumuchitila Khristu , tangoyerekezani , tikaganizira iwo amene tikuwatumikila monga Khristu- tingawatumikile bwanji? Kodi zifunika motani?. Tikuyenera kuthandiza anthu kuona chimenecho , pamene akutumikila dera lawo , akutumikilanso Khristu.

6. GWIRANI NTCHITO LIMODZI

Tawerengani ka nkhani kali mmusika.

Kwa zaka zambiri , mpingo wakhala ukudabwa kuti munthu amene anatumidwa kusamala pa tchalichi amangosinthidwa pafupi pafupi. Wina wake amazipeleka ndi kenako , kwa miyezi itatu kapena folo. Amanena kuti basi sakufunanso kuchita ntchito. Anthu ambiri amazipeleka mu Madera ena a zifunika kwawoko koma amakhazikika kwambiri zaka zingapo. Kodi tsopano anthuwa samakhalitsa chifukwa chiyani pa ntchito yawoyi ? ozipelekawo anafunsidwa kuti ndi chifukwa chiyani amachoka , koma ambiri mwa iwo amakana kuyankha mayankho olondola. Munthu wina anapeleka chiganizo , mwina akhale ndi anthu amene amayang'anira zinthu , mwina zikhoza kukhala bwino . Mpingo unaganiza kuti kunali koyenera kuyesa , ndipo gululi linakonzedwa.

Lero lino , pali gulu la anthu azibambo ndi ana amene akugwira ntchito pa gulu liimeneli. Amakumana limodzi loweruka lina lililonse mmamawa 7 koloko . amayamba ndi pemphero kenako ndikupita ku Madera awo ena ndi ena amene akuyenera kukagwirako ntchito limodzi- awiri kusengela mitengo , awiri kusesa , 9 koloko mmamawa. Amamwa onse khofi ndikuonetsana za mmene zinthu zikuyendera mmoyo mwawo. Wina aliyense ali ndi mwayi ogawila ena za zimene akuziona kuti ndi mwayi, ndipo amamalizitsa ndi pemphero.Kenako amachoka onse limodzi. Amapuma pokhapokha ngati alibe mphamvu zogwirila ntchito kapena ali ndi zina zomwe akuyenera kuzichita.

KAMBIANANI:

- Kodi ndi chani chomwe chinapangitsa anthu ozipelekawo kuti azifuna kugwira ntchito kwa nthawi yaitali?.
- Kodi mukuganiza ngati kugwirila ntchito limodzi kumathandiza bwanji?.
- Kodi ndi zinthu zina ziti zomwe anapanga kuti pakhale umodzi?.
- Kodi pali ziganizo zina ziti zomwe tingathe kuganizila kuti anthu atumikile pamodzi?.

7. Pangani Ntchitoyo ikhale yosangalatsa

Anthu amachita zinthu kwambiri zomwe iwo amasangalala akamazichita! Amagwira ntchito kwa nthawi yaitali ndikukhala otanganidwa akamasangalala ndi chimene akuchita. Nthawi zina timaganiza ngati a khristu akuyenera kutengedwa mwa siliyasi, koma baibulo limanena za chimwemweme. kumwamba kudzadzadza ndi chimwemwe ndi msangala.

KUKAMBIRANA KWA MMAGULU ANGONO ANGONO

Malangizo kwa Mphunzitsi: GWIRITSANI NTCHITO **BUKHU LA OPHUNZIRA.**

- Kodi mwayesera njira ina mwa zimenezi?. Kodi ndi chani chomwe chagwira? Kodi ndi chani chomwe sichinatheke?.
- Kodi ndi ndime zina ziti zomwe tingagwiritse ntchito kuti tiphunzitse za ubwino wa ntchito?.
- Kodi ndi njira zina ziti zomwe mwagwiritsa ntchito kuti muzindikile ndi kuthokoza anthu? Kodi ndiziganizo zina ziti zomwe mungayesere?.
- Kodi mungapange motani kuti ntchito ikhale yosangalatsa?. Kodi ndi njira zanzi zomwe mungapangitsire kutumikila kukhala kosangalatsa?.

KUPELEKA LIPOTI

Malangizo kwa Mphunzitsi: Onetsetsani kuti kalasiyi muipatse nthawi yokwanila kuti muyankhe mafunso pamene mukupeleka lipoti.

CHOCHITIKA CHA MMAGULU AKULUAKULU

Tinangoona chabe njira zisanu ndi ziwiri zimene anthu amalimbikitsika pamene akutenga nawo mbali mu kutumikila: Kuphunzitsa, kukonza mwayi, kuitanila anthu kuti atenge nawo mbali, kuwazindikila, kugwirila ntchito limodzi, kunva kuti iwo ndiofunikila, ndi kusangalalanso.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Funsani wina aliyense kuti abwere kutsogolo ndikuloza zinthu zitatu zomwe zingakhale zokopa mtima kwa iwowo.

- Kodi wina aliyense anasankha njira yomweyo? Kawirikawiri adzakhala osiyana.
- Fotokozani kuti anthu onse amakopedwa mtima, ndiye mu mipingo yathu, tikuyenera kuika pulani imene imakopa mitundu yonse ya anthu.
- Kodi pali ena amene apeza malikisi abwino?. Kodi mukuganiza ngati amenewa anapeza malikisi abwino kuposa anzawo chifukwa chiyani? Kodi pali njira zina zomwe mungagwiritse ntchito kulimbikitsa anthu a mu mpingo mwanu?.

MPINGO OMWE UMATUMIKILA

Ngati tikufuna kuti mipingo yathu itukuke, machitidwe a zinthu mmoyo mowirikiza (osangoti kamodzi kokha pa ka nthawi), ndiye kuti choyamba tizipeleke ku kupempherera mpingo wathu. kenako tikuyenera tsopano tilankhule chimene tikhodza kuchichita, ndikukondwera ndi ntchito za chikondi pafupi pafupi. MMvetserani ka nkhanu aka ka mpingo umene unalimbikila kwambiri kugwira ntchito ndikupangitsa ntchito za chikondi kukhala moyo wawo wa tsiku ndi tsiku ku mpingo wawo.

Abusa a James amamva kugonjetseka pangono mkati mwawo. amadziwa kuti akufunika anthu kuti azitumikila mu mpingo wawo, koma samadziwa kuti apange bwanji. mzawo anawapatsa nambala ya foni ya abusa Mose ndipo anapeleka chiganizo chokuti amuimbile kuti ampatse malangizo. Ndipo iwo anawaimbiladi abusa Mose ndipo atatha kulankhula kwa ka nthawi kochepe, anauza kuti akuyenera kuti aike chikhalidwe cha kutumikila pa mpingo wawo. Abusa a James anavomereza ndithu kuti analibe ganizo kuti kodi chikhalidwe chotumikila ndiye chitii. “musadandaule”. Abusa Mose anayankha, “Nati inenso sindimadziwa kufikila zaka zingapo zapitazo, pamene ndidabwera ku sevisi ina yake imodzi, ndipo ndi kuonetsani chimene ndikutanthauza.

Abusa Mose anakumana ndi abusa James polowera mkachisi . anali omasuka ndi okondwera poona kuti abusa Mose akufunitsitsa kwambiri kuti amuthandize ndithu moona mtima osati kudzangomuonetse chabe mpingo wake waukuluwu.

Mmene amalowa mkachisi , abusa JAMES Anaona positala yaikulu “ imene inalembedwa kuti , “Thandizilani mu tsiku la kugwira ntchito pa malo pano” Pansi pake panalembedwanso vesi “..koma inu abale , musatope ndikuchita ntchito zabwino- 2 atesalonika 3:13”. Mwezi wina uliwonse umalembedwa ndi ma laini pafupi pake . laini yoyamba inali yolembe ntchito zachikondi zingati zomwe mwachita , laini yachiwiri inali yolembe anthu amene anagwira mwezi umenewo , ndipo laini yachitatu inali yolembe kuchuluka kwa anthu amene anathandiza nawo pa ntchitoyo.

‘Kodi ichi ndi chani?. Anafunsa abusa James.

‘Timakhala ndi tsiku lakugwira ntchito mwezi ndi mwezi , abusa a mose anafotokoza , ‘ pa masiku amenewo timayetsesa kuitana anthu ochuluka mmomwe tingathere ku mpingo mu njira ina iliyonse yomwe tingathe. Ndimafuna anthu alembe pamene ndili kutsogolo kulalikila , ndipo anthu a mu mpingo amakauzanso anzawo ena amene amakumana nawo tsiku ndi tsiku. Ena a mu mpingo amasamala mminda , kapena kupenta makoma. Ena amatumikila mdera kukonza nyumba ena kupanga tsiku lachikondwerelo cha ana. Tili ndi ma positala ambiri kuzungulira kachisi amene amakumbutsa mpingo za masiku amenewa ndikuona za kuti ndi anthu angati amene akugwira ntchito ndiponso kuti tikuwafuna kuti akhale otenga nawo mbali . mwezi wina uli wonse , timalembanso za ntchito zachikondi zomwe tagwila , anthu angati amene anathandiza nawo , komanso ndi anthu angati amene athandizika nawo. Mwezi wina uliwonse , timayetsesa kuonjezera anthu amene akuthandizila nawo.

Abusa a James anayangana kuzungulira kachisiyu , ndipo anaona kuti zinthuzi zinali zoona- panalidi ma positala ambiri amene anali ndi ma vesi ochuluka pakhoma . Pakhoma la kumbuyo , panali zithunzi zambiri za anthu ambiri amene akugwira ntchito mu zinthu zomwe zimachitika mbuyomo. Panali zithunzi zambiri za anthu amene amatenga nawo mbali mu zinthu zosiyanasiya , kumanga manyumba , kukonza msewu , kusamala kachisi , ndikuphunizitsa ana , “ Tiyeni timange tonse ufumu wa Mulungu.’

Abusa a James anakhala panso pamene abusa mose anayamba kukatumikila mu sevisi. Abusa James anazindikila kuti panali anthu ena amsangala amene amapeleka moni kwa anthu onse , ndipo panali ena amene amathandiza mzimayi wina amene samaona , kumulondolera pokhala ndikumupezera mpando ndikumawapasanso kapu ya tiyi. Ananva kulandilidwa kwakukulu kwambiri mu mpingowu ndipo anaganiza kuti nayenso akachite zomwezo ku kachisi kwawo.

Sevisi itayamba , achinyamata anachita zamasewro ndipo mpingo wonse unayimbila limodzi nyimbo. Patatha kulambila , abusa mose anaitana anthu kuti akapeleke umboni . Mzimayi wina wachikulire anadzuka ndikupelekele umboni. Umboni wake unali motere: “ amuna anga anamwalira ndipo pano ndikusamalira zizukulu mwa ndekha . Nyumba yanga inali itaonongekeratu ndipo imachucha kwambiri ndipo azukulu angawo samakhodza bwino kusukulu. Mwadzidzidzi , anamwetulira ndikunena kuti mpingo wandithandiza kukonza denga la nyumba yangayi . komanso anyamata ena anamuitana mzukulu wanga kukhala mbali imodzi ya maphunziro cholinga choti asalephelenso ayi!Ndili othokoza kwambiri ndi mmene mpingo wachitila pondisamalira. Ndipo wina aliyense anali odabwitsika kwambiri.

Zikomo nonse! Wina aliyense anasunthika ndi umboniwu. Abusa Mose anabwerela kutsogolo ndikuitana anthu amene anamanga nyumba ya agogowa , komanso anyamata amene anamuphunzitsa mzukulu wawo aimilire. Pamene amaimilira , mpingo onse unawaombela mmanja. Iwo anali okondwa ndipo anakhala panso mwachangu.

Abusa a Mose anapempherela mzimayiyu ndi anthu onse amene amathandizirawo- kumuthokoza Mulungu chifukwa cha kufuna kwawo kumubweretsera Mulungu ulemelero kudzera mu ntchito zawo za chikondi. Anawalimbikitsa kuti palibe chiwalo china chilichonse cha mpingo chomwe chilli chopanda ntchito , ngati pali

ziwalo zina za thupilo , ndiye kuti thupi lonse silikugwira ntchito. Anafunsa iwo amene analembetsa kale kuti aonetsetse kuti afunse wina wake kuti adzakhale nawo pa tsiku la kugwira ntchito.

Pamene seviisi imapitirila , abusa James anaganizila kuti zonse zomwe anaona ndi kumva . kodi zinali zodabwitsa kuti anthu ambiri amalimbikila mu ntchito ya chikondi pafupi pafupi?. Kenako anamvetsetsa zomwe Abusa mose amatanthauza mmene amati ” kukonza danga la kugwira ntchito”.

KUKAMBILANA KWA MMAGULU ANG’ONO ANG’ONO

Malangizo kwa Mphunzitsi: Gwiritsani ntchito **BUKHU LA OPHUNZIRA**.

- Kodi njira zisanu ndi ziwiri zolimbikitsira, zikuimilidwa bwanji mu nkhaniyi?.
- Kodi ndi ziganizo ziti zina zomwe mwaphunzira zomwe zikhoza kukagwiranso mu mpingo wanu?.

MATHERO

Aefeso 4 imati : ” Thupi lonse ... limakula ndipo limazimanga longa mwachikondi mmene chiwalo chakenso chimachitira.” Timakula pamene tikupatsidwa mwayi kuti tigwiritse ntchito mwayi oti tionetsere mphatso zathu! Monga atsogoleri tikufuna tilimbikitse mpingo wonse kuti ukhale nawo mu kugwira ntchito.

KUUNIKILA PAWEKHA.

Tayang’ananinso pa njira zisanu ndi ziwiri zakulimbikisira anthu ena kugwira ntchito ndi ziganizo zomwe zakonzedwa mu magulu amenewa. Kodi ndi zinthu zitatu ziti zomwe mukufuna kuzigwiritsa ntchito mwezi uno kuti mubweretse anthu ambiri mu mpingo mwanu kuti azigwira ntchito?.

Malangizo kwa Mphunzitsi: Malizani ndi kutengapo nthawi kupempherera mipingo yawo komanso wina ndi Mzake.